


WAMKULU KUPOSA

SOLOMONI ALI PANO

 Zikomo inu, mochuluka kwambiri. Usiku wabwino, abwenzi. Wokondwa kukhala pano usikuuno, ndikungosangalala ndi kugwirana chanza ndi kuyanjana ndi mzanga wakale, M'bale G.H. Brown. Ine sindinamuwone kwa zaka. Iye ndi mmodzi wa anga—azimzanga oyambirira, ku Arkansas, pamene ife tinali pa 505 Victor Street kumeneko.

² Ine ndikukumbukira, M'bale Brown, usiku umene dona kumusi mu chipinda chapansi, kumbuyo kwake, akukwawa pa nsana wake, ndi iye... Anabalalika mmalingaliro ake, ndipo iye ali mu chikhalidwe choipa kwambiri. Kenako, ine ndinakamupeza iye cha ku Jonesboro kwinakwake, akuganiza bwino bwino, ali ndi mwamuna wake, ndipo ali bwinobwino basi monga iye akanakhalira.

³ M'bale anangokumana nane kuno, ndinangogwirana chanza ndi dzanja lake. Iye anali kuyankhula za kukhala mmalo ena ake, mkazi wake anali ndi khosi lotupa, ine ndikukhulupirira, pa mmero wake. Iye anachiritsidwa mu msonkhano. Iye akadali wochirabe.

⁴ Mulungu ndi wodabwitsa, sichoncho Iye? Ndife othokoza kwambiri chifukwa cha zimenezo. Ife tiyenera kukhala, chimene ife tiri, anthu okondwa kwambiri mdziko lapansi, ndi anthu a Mulungu, osasamala, mu njira yakuti ife sitimawopa imfa. Inu mukudziwa, Khristu anagonjetsa chirichonse, ngakhale imfa, ngakhale mantha a imfa. Eya. “O imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma mathokoza akhale kwa Mulungu Amene amatipatsa ife chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Momwe ife timamukondera Iye chifukwa cha zimenezo!

⁵ Mlongo wamng'ono uyu wochokera ku Florida, ine ndikukhulupirira, iye anati, kapena kwinakwake kuno, amene anaimba nyimbo ija: *Kutsika Kuchokera Ku Ulemelero Wake*. Imeneyo ndi nyimbo yanga yoikonda, inalembedwa ndi mzanga, M'bale Booth-Clibborn. Ine ndikuganiza iyo ikufotokoza kwenikweni Umulungu Wake wapamwamba lero, mu tsiku limene anthu akuyesetsa kumupanga Iye mneneri chabe kapena—kapena mtsogoleri wina. Ndipo ine ndikuganiza kuti iyo imafotokoza chimene Iye ali, ndipo ine ndimaikonda kwenikweni nyimbo imeneyo.

⁶ Tsopano, inu mukudziwa, ndipo chotero gawo loipa la zinthu izi, misonkhano iyi si yaitali mokwanira. Ife timangofika

pokumana wina ndi mzake, ndi kuti “moni,” ndipo kenako nkumasiyananso. Koma ndithudi ndakhala ndikuyembekezera kuti ndidzabwerenso kuno.

⁷ Ine ndikuuzani inu chinachake chaching’ono. Ine sindinanene icho kwa kwa lingaliro usiku wina, za ine kukhala ndi chidebe cha manyuchi a mapira amene chimbalangondo chaching’ono chija chinalowamo. Koma winawake usikuuno anandibwezera ine, iwo ananditumizira ine mtsuko wa manyuchi a mapira. Zikomo inu, ndipo ndiwonetsetsa kuti chimbalangondo chisapeze zimenezo. Ine ndimufunsa mkazi wanga kuti akandiphikire mbale yodzaza mabisiketi, ndipo ine ndikalowa kumene mmenemo. Inde, bwana, ine ndithudi ndimawakonda mapira.

⁸ Billy, mwana wanga, wangonduza kumene ine, anati, “Adadi, iwo anakutengerani inu chopereka chachikondi.”

⁹ Ine ndinamuza mlaliki uyu kuti ine sindimafuna zimenezo. Mwaona, ine sindinabwerere zimenezo, anthunu. Ine ndabwera kuti ndidzakuthandizeni inu, kudzayera kuteru. Koma palibepo njira yoti ine ndingabwezere zimenezo. Ndipo ngati aliyense akumudziwa aliyense pano ali moyipa kwenikweni, winawake, mkazi wamasiye kapena chinachake, iwo ali nacho icho. Chotero zikomo inu mochuluka kwambiri. Inu mukudziwa, Baibulo linati, “Mochuluka monga inu mwachitira kwa aang’ono,” ameneyo ndi ine, “aang’ono awa, inu mwachitira izo kwa Ine.” Ndipo ine ndikupemphera kuti Mulungu akudalitseni inu chifukwa cha zimenezo, ndipo kuti Iye atero—Iye atero. Ine ndikuuzani inu, ngati palibe munthu yemwe wavutika, kuti atenge icho, ine ndikachiyika icho ku ntchito ya umishonare ku maiko akunja. Ine ndimapitako, ndekha, kuchitira kuti ndidziwe kuti zagwiritsidwa ntchito moyenera.

¹⁰ Ndipo kotero ndiye kuyesetsa kubweretsa Uthenga wodabwitsa uwu wa—wa chisomo cha Mulungu umene wabweretsedwa kwa ife mmasiku otsiriza ano, Uthenga, mopambana mmene ine ndikudziwira momwe ndingawubweretsere Iwo, ndipo ndi Uthenga womwewo umene ine ndinalalikira zaka zambiri zapitazo. Ine sindinachoke kwa iwo inchi imodzi, chifukwa iwe sungathe. Ngati ine ndikanatero, ine ndikanayenera kuti ndichoke mu Baibulo. Mukuona? Chotero izo ndi zochokera mu Baibulo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo Ahebrei 13:8 amati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ine ndimakhulupirira zimenezo.

¹¹ Tsopano, ine ndinali kuyankhula kwa inu lero, masana, pa Uthenga Wabwino. Ine ndinali wokondwa kumuwona M’bale Tracy Boutliere pano, ndi m’bale uyo cha kuno. Ndipo, ine, ndipo

inu mukudziwa momwe ine ndikumverera kuyima pano? Ine—ine ndikukhala ngati ndikuchokako kukulalikirira kumeneko usikuuno, pa chifukwa cha atumiki abwino onse awa akhala pano. Chotero ine ndingoyankhula pang’ono za Ambuye Yesu, pa Lake, vumbulutso lalikulu la Iye lero, ndi za mphamvu Yake yochiritsa odwala.

¹² Ndipo mwana wanga anabwera, kanthawi kapitako, ndipo iye anadzapereka makadi ena a pemphero, ndipo ife tikufuna kuti tiwapempherere odwala usikuuno. Ndipo inu muli naye mwamuna pano yemwe akhoza kulalikirira Uthenga; iwo ali nawo, sabata yonseyi. Ndipo ine ndiri pano kuti ndidzayesetse kuchita gawo langa, kudzasonyeza kuyamikira kwanga chifukwa cha kudzipereka kwanu kwa Yesu Khristu, popempherera odwala.

¹³ Ndipo tsopano ife tisanatsegule Bukhu, tiyeni tiyankhule kwa Mlembi wa Bukhu.

¹⁴ Nthawi ina kale, panali munthu ananena kwa ine. Ine ndinali kuyankhula za phunziro linalake mu Baibulo, ndipo ilo linali phunziro lakuya kwambiri limene pamakhala mtsutsano wochulukira, ndi pa Logos, ndi zina zotero. Ndipo iye—iye anayang’ana pa ine. Ndipo ine ndinali ndi M’bale Jack Moore, ndipo tinali tikubwera uko ku Cross Lake, mu Shreveport, Louisiana. Ndipo munthu uyu anandiyang’ana ine, ndipo iye anati, “Iwe sumalidziwa basi Baibulo lako.”

¹⁵ Ine ndinati, “Koma ndimamudziwa Mlembiyo mwabwino kwenikweni. Ndipo ine ndikutsimikiza, ngati ndikumukonda Iye ndi kumudziwa Iye mwabwino kwenikweni, Iye adzawulula Mawu Ake kwa ine.”

¹⁶ Chotero tiyeni ife tiyankhule kwa Mlembiyo tsopano, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. Tsopano pamene ife tikukhala chete. Ndipo, kumbukirani, mmitima yathu tsopano, kodi chiripo chopempha usikuuno pakati pathu, chimene inu mukufuna kuti Mulungu akumbukire, kuti inu mukupempherera chinthu chinachake ichi, mwinamwake wokonedwa kuti abwere kwa Khristu, usikuuno, mwinamwake winawake kuti achiritsidwe, kapena chopempha china? Muchigwire icho mmalingaliro anu, ndipo mukwezere mmwamba manja anu kwa Mulungu, nenani, “Ambuye, mukumbukire chopempha changa.” Ndizo zonse, kulikonseko. Ndi dziko losowa bwanji ili!

¹⁷ Ambuye Yesu, ife tikubwera kudzakuyandikirani Inu mu Dzina lokwanira mu zonse ilo, podziwa ichi, kuti ife tinalonjezedwa kuti mapemphero athu adzamvedwa. Munati, “Chimene inu mudzapempha mu Dzina Langa, icho chidzaperekedwa.” Ndipo ife tikubweretsa zopempha zonse izi, usikuuno, pamaso pa Mpandowachifumu woyera waukulu wa ngale pamene Nsembe Yamagazi ili, Amene amakhululukira

machimo athu onse, ndipo amachiza matenda athu onse. Ndipo ndife oyamikira kwambiri kwa Inu, usikuuno, chifukwa cha mwayi waukulu uwu umene ife tiri nawo, ndi Mawu a Mulungu, amene sangakhoze kulephera. Ngakhale Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, Mawu sangakhoze kulephera konse. Ndipo Mawu ndi Mulungu. Ndipo Iye analonjeza kuti Iye adzamva ndipo adzayankha zopempha zathu. Tsopano ife tikutsimikiza kuti ife tapeza zimene ife tikuzipempha. Ndipo dzanja langa liri mmwamba, inenso, Ambuye. Yankhani, usikuuno, zopempha zathu.

¹⁸ Ife tikufuna kuti tikuthokozeni Inu chifukwa cha chimene Inu mwakhala kwa ife, mu msonkhano waukulu uno, kubwerera kudutsa mmoyo. Ndipo ife nafenso tikukuthokozani Inu pa chimene Inu muli kwa ife, kuti mudzakhale mtsogolo. Ndi mu ora la imfa yathu, ngati Inu mutachedwe, ife tikudziwa kuti Inu mudzakhala—ngalawa yakale ya Zioni, Inu mudzakhala Mapiko onyezimira, Inu mudzakhala Nyenyezi ya Mmawa imene idzawalitsa chigwa cha mthunzi wa imfa, Inu mudzakhala Mmodzi yemwe ati adzatinyamule ife kuwoloka mtsinjewo, kukalowa mu Dziko lolonjezedwa lalikulu ilo. Ife tiri okhutitsidwa ndi zimenezo, Ambuye.

¹⁹ Usikuuno, pakati pathu pakhala amuna, a imvi ndi wowerama ndi ukalamba, ndipo zaka zambiri zapitazo pamene ine ndinali mnyamata wochimwa, ndinali nditaima pa ngodya za msewu ndi kumamenyana ndi kumenya kwabwino kwa chikhulupiriro, chifukwa cha Uthenga womwewu umene ife tikuyesetsa kuwumenyanira usikuuno. Atate Mulungu, ndife oyamikira amuna awa akadali moyo, monga maumboni a chikhulupiriro chachikulu ichi chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera. Mulole ife tizimenyera izo nthawizonse ndi kukhala okhulupirika ku malo athu a ntchito, mpaka Yesu adzabwere.

²⁰ Tsopano ife tikukupemphani Inu kuti muwadalitse Mawu amene ife titawerenge, ndi zimene titanene usikuuno. Mulole Iwo agwere mu nthaka yachonde yomwe iti idzabale utumiki, kuti pasakhale wochimwa mmodzi mchipinda chino, yemwe ati achoke pano, amene sadzapulumutsidwa. Mulole munthu wodwala aliyense achiritsidwe. Mulole pasakhale munthu mmodzi wofooka pakati pathu pa mapeto a msonkhano. Ine ndikudziwa kuti ilo ndi phiri lalikulu limene limaima patsogolo pathu. Koma Inu munanena mu Uthenga Wanu, molingana ndi Marko Woyera 11:22, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zimene inu mwanena zifika pochitika, inu mudzakhala nazo zomwe inu mwanenazo.” Tsopano ife tikukhulupirira zimenezo.

²¹ Inu munati, “Pamene inu muima kupemphera, mukhulupirire, mukhululuke.” Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutikhululukire ife zolakwitsa zathu, monga ife

tawakhululukira iwo amene atilakwira ife, kuti pasakhale chinthu chimene cholepheretsa mapemphero athu kuti ayankhidwe.

²² Ndipo, Ambuye, mulole, ngati zitachitika kuti sitidzakomane konse kachiwiri monga chonchi mu msonkhano wina, mwinamwake chaka kuchokera pano kapena paliponse pamene izo ziti zidzakhale, ife tikudziwa kuti kukubwera msonkhano umodzi waukulu umene ife tonse titi tidzakakhale kumeneko, ndipo umenewo ndi Mgonero wa Chikwati. O Mulungu, mulole pasadzakhale mmodzi wa ife akusowa pa nthawi imeneyo. Kufikira nthawi imeneyo, tisungeni ife athanzi ndi okondwa, kuti tizikutumikirani Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupempha izi. Amen.

²³ Tsopano, kuti tipempherere odwala, ine—ine sindimatengeka ndi kulalikirira. Monga ine ndanena, ndi—ndi kudzoza kosiyana; Mzimu womwewo, mpita chabe wosiyana umene iwe ukuyendamo.

²⁴ Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge gawo lodziwika la Lemba, ndipo Malemba pang'ono apa ine ndikufuna kuti ndilozereko, basi ife tisanaitane mzere wa pemphero. Ndipo ine ndikudziwa kuti kwatentha, ndipo ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalikitsa.

²⁵ Ndipo ine ndikudziwa kutsekera kwa msonkhano, sabata lalikululu, ndi momwe inu nonse mwadzazidwira mpaka pamapeto tsopano, ndipo mukupita kunyumba kuti mukakhale ndi nthawi yopambana. Sindikufuna mupite kwanu kuti mukangokhala ndi nthawi yopambana kusangalala nawo madalitso a Mulungu, koma mupite kwanu kuti mukatenge zomwe inu mwaphunzirazi ndi kuzipereka izo kwa winawake. Ndipo mulole ana a msonkhano uno, amene abadwa mwatsopano, mu msonkhano uno, chaka cha chamawa mudzabwere ndi zidzukululu-zidzukululu-zidzukululu-zidzukululu limodzi nawo; kutanthauza kuti inu mwamupindulira winawake, ndipo iwo amamupindulira winawake, ndipo iwo amupindulira winawake kwa Ambuye.

²⁶ Tsopano tiyeni titsegule usikuuno ku Marko Woyera, mutu wa 12. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyambe kuwerenga kuchokera pa ndime ya 38 ya Woyera. . . ya Marko Woyera 12, kuwerenga motsika ndi ndime ya 42, kuphatikizapo. Ndipo, kawirikawiri, monga mwa mwambo nthawi zambiri, ife timaima pamene ife tikuwerenga Mawu a Mulungu, koma pokhala kuti inu mwalongezedwa kwambiri usikuuno, ife tilumpho zimenezzo, ndipo mungokhala molemekeza ndi kumamvetsera ku Mawu. Ngati inu muli nalo Baibulo, nditsatireni ine pamene ine ndikuwerenga.

*Ndiye ena a alembi ndi a Afarisi anayankha, anati,
Ambuye, ife tikufuna tiwone chizindikiro chochokera*

kwa inu.

Koma iye anayankha nati kwa iwo, M'badwo woipa ndi wachigololo ukufunafuna chizindikiro; ndipo apo sipadzakhala chizindikiro... choperekedwa kwa iwo, koma chizindikiro cha mneneri Yonasi:

Pakuti monga Yona anali masiku atatu ndi usiku utatu mmimba mwa chinsomba; chomwechonso Mwana wa munthu adzakhala masiku atatu ndi usiku utatu mu mtima wa dziko lapansi.

Amuna aku Nineva adzawuka mu chiweruzo ndi m'badwo uno, ndipo adzawutsutsa iwo: chifukwa iwo analapa pa kulalikira kwa Yona; ndipo, taonani, wamkulu kuposa Yona ali pano.

Mfumukazi ya kummwera idzawuka mu chiweruzo ndi m'badwo uno, ndipo idzawutsutsa iwo: pakuti iye anabwera kuchokera ku mbali zakutali za dziko lapansi kuti adzamve nzeru za Solomoni; ndipo, taonani, wamkulu kuposa Solomoni ali pano.

²⁷ Ine ndikhoza kugwiritsa ntchito iyi kwa mutu: *Wamkulu Kuposa Solomoni Ali Pano.* Ngati titawerenga zigawo zakumbuyo za Lemba, patsogolo pa izi, ife tipeza kuti zikulumikizana ndi zomwe timanena usiku wathawu.

²⁸ Pamene Khristu anabwera pa dziko lapansi, Iye anabwera kwa Ake Omwe, ndipo Ake Omwe sanamulandire Iye ayi. Ndipo Ayuda amenewo ankalangizidwa ndi Malemba, za mtundu wanji wa khalidwe limene Mesiya akanadzakhala. Ndipo Mesiya anali woti adzakhale mneneri, molingana ndi malamulo awo. Mose anati, “Ambuye Mulungu wanu adzautsa Mneneri, wonga ine, ndipo kwa Iye anthu adzakangamirako; ndipo ngati sadzamumvera Iye, iwo adzadulidwa kuchoka kwa anthu.”

²⁹ Mwaona, Lemba silimasiya konse m'badwo uliwonse popanda kudzindikiritsidwa komveka bwino, kuti ife tikhoze kudziwa ora lomwe ife tiri kukhalamo.

³⁰ Ngakhale mu Mateyu Woyera 24, Yesu akuyankhula za nthawi yotsiriza, Iye anati, “Tsopano phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu.”

³¹ Ndipo Iye anati chidzakhala chiyani chizindikiro cha mafunso atatuwo. “Kodi ndi liti zidzakhale kuti sipadzakhala mwala umodzi udzasiyidwe pamwamba pa umzake, wa nyumbayo? Kodi chizindikiro cha Kudza Kwanu ndi chiyani, ndi mapeto a dziko lapansi?” Ndipo Iye anayankha mafunso atatu onsewo. Nthawi zambiri, anthu amawayika atatu onsewo ngati funso limodzi, koma iwo anamufunsa Iye mafunso atatu. Iye anawayankha mafunso atatu amenewo. Koma Iye anapereka, motsatira pamenepo, chizindikiro, chifukwa, Ayuda amafunafuna chizindikiro. Ndipo nchifukwa chiyani

iwo amafunafuna zizindikiro? Ndi chifukwa chakuti iwo anaitanidwa kuti adzachite chomwecho. Myuda nthawizonse ankakhulupirira mu chاوزimu.

³² Ngakhale pansi pa lamulo, kuti pamene pakhala wolota, kapena mneneri, amene apereka uthenga umene ukhala wosamvetsetseka pang'ono, kapena iwo sanali otsimikiza kwambiri za zimenezo, iwo amakhala nayo njira yopezera ngati uthenga umenewo unali wolondola kapena ayi. Iwo ankatenga wolota uyu, kapena mneneri, kupita naye ku kachisi kumene—Urimu ndi Tumimu, icho chimakhala chapachifuwa chimene chinkapachikika, kapena chimakhala pa chifuwa cha Aaroni, chimene chinkaimira mafuko onse a Israeli. Ndipo mneneri uyu ankalosera, kapena wo—wolota ankanena loto lake.

³³ Ndipo zinalibe kanthu momwe zinkawonekera zenizeni, ngati loto limenelo kapena uneneri umenewo sunyezimiritsa kuwala kwauzimu, kukhala ngati kusakanizikana monga utawaleza kudutsa pamenepo, chimene chinkatchedwa Urimu ndi Tumimu, uthengawo unkakanidwa. Chachirengedwe chiyenera kuyankha mwa chاوزimu, ndipo chاوزimu chiyenera kuyankha mwa chirengedwe. Chotero, mu Chipangano Chakale, Urimu ndi Tumimu amakhala choyezera, ngati mawuwo anali owona kapena ayi. Izo zinali pansi pa unsembe wa Levitiko.

³⁴ Koma Mulungu sanatisiye ife opanda Urimu ndi Tumimu, chifukwa Mawu Ake usikuuno ndi Urimu ndi Tumimu. Ziribe kanthu momwe uthenga ukumvekera bwino, kapena momwe lotolo likumvekera bwino, komabe ngati iwo sathwanima kudutsa Urimu ndi Tumimu, Mawu a Mulungu, langizo langa: Zisiyeni izo zokha, chifukwa Mulungu samachitira umboni. Chifukwa Bukhu ili ndi vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu.

³⁵ Tsopano, Yesu anali atabwera ndipo anali atachita chimodzimodzi basi monga Malemba anati Iye akanati adzachite.

³⁶ Ndipo pamene mtumwi Petro, monga ife tinalankhulira usiku wathawu, polangizidwa ndi abambo ake, ndi aziphunzitsi, kuti padzakhala kuwuka kwa Mesiya, ndi kuti Mesiya ameneyo akanadzakhala Mneneri. Tsopano kwa zaka foro handiredi, kuyambira pa Malaki, iwo analibe aneneri. Ndipo apa panali Munthu amene pamene Iye ankayenda, sikuti anavala mosiyana mulimonse, osati monga wansembe wina wodziwika bwino kapena mlaliki, koma munthu wamba chabe. Ndipo iye sakanamudziwa Mesiya uyu momwe Iye anavalira, koma iwo akanamudziwa Iye mwa—Moyo umene unali mwa Iye. Ndipo pamene Yesu anayang'ana pa iye ndipo anati, “Dzina lako ndi Simoni ndipo ndiwe mwana wa a Yonasi,” ndiye mtumwiyo anali wokonzeka kuti agonjere, chifukwa chakuti iye anadziwa kuti Yesu sanamudziwe iye. Osati kokha kuti Iye anamudziwa

ieye, koma Iye anawadziwa abambo ake nawonso, kotero iye anadziwa kuti icho chinali chizindikiro cha Mesiya.

³⁷ Iye tinamutsatiranso Filipino, kuti tikamupeze Nataniele. Tinamubweretsa iye uko, yemwe anali a—munthu wokhazikika, wophunzira kwambiri mu Lemba. Iye tikupeza kuti mwinamwake Filipino anamulangiza iye, pa msewu akupita, chimene chinali chitachitika. Koma pamene iye anafika kwa Iye, Iye anamuitana iye, anati, “Taonani wachi Israeli, mwa yemwe mulibemo chinyengo.”

Iye anati, “Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine, Rabbi?”

³⁸ Anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, ine ndinakuwona iwe.”

Ndipo iye anati, “Rabbi, Ndinu Mwana wa Mulungu, Mfumu ya Israeli.”

³⁹ Ndiyeno ku fuko la Msamariya, kumeneko mkazi wamng’ono uyu ku Sukari. Momwe kuti iye mu chikhaliidwe chake monga mkazi wa mbiri yoyipa; koma pamene Kuwala kwa Uthenga kuja kunafalikira pa njira yake, ndipo Iye anamuuzza iye za tchimo lake ndi zomwe iye anali atachita, iye anati, “Bwana, Inu muli, muyenera kukhala mneneri. Ndipo ife tinalangizidwa, ndipo ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu.” Chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya.

⁴⁰ Ndiye ife tinaphunzira kuti Iye sanachite chizindikiro chimenecho pamaso pa Amitundu, koma ananenera kuti izo zikanadzachitika kuno mmasiku otsiriza, mwa Mzimu Woyera. Ndipo, kuwuchitira mwano Iwo, kukanakhala zosakhululukidwa.

⁴¹ Monga Iye anati izo zikanadzakhala monga izo zinali mmasiku a Sodomu, pamene ife tinapeza kuti choyimira cha Mulungu mwa munthu, munthu wokhalapo, amene anadya nyama ya ng’ombe yokalamba, kapena kamwana ka ng’ombe, kani, ndipo anamwa mkaka kuchokera kwa ng’ombe, ndipo anadya mkate, ndipo iye anamutcha Iye, “Elohim,” Mulungu wamkulu, Mlengi.

⁴² Mulungu anapangidwa thupi mmawonekedwe a Yesu Khristu.

⁴³ Ndipo lero Iye ali mu mpingo Wake, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, akadali Mulungu. Ndipo munthu ameneyo mu thupi, anaimiridwa pa nthawi yotsiriza dziko la Amitundu lisanawotchedwe ndi moto, kuti Mulungu akanadzakhala mu mnofu wa munthu, akuchita chinthu chomwecho, kuti adzadzitsimikizire Iyeyekha kwa Amitundu. Ndipo ife tinamuwona Iye atabwera pakati pathu, usiku watha, ndi kudzachita chinthu chimenecho.

⁴⁴ Chotero tsopano Yesu anali akuwadzudzula anthu awa, usikuuno, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo, chifukwa iwo

akanayenera kuphunzitsidwa Mwamalemba. Koma miyambo ya tsikuli inali itawakoka anthu kuchoka mu Baibulo, Lemba. Yesu anati, “Inu ndi miyambo yanu mwapanga Malamulo a Mulungu kukhala opanda mphamvu.”

⁴⁵ Ndipo ine ndikudabwa usikuuno, ngati Iye ataima pa nthaka iyi ya United States, ngati Iye sanganene chinthu chomwecho kwa ambiri usikuuno. Ndi miyambo ya anthu, inu mwatenga Malamulo a Mulungu ndipo mwawapanga iwo kukhala opanda ntchito, polalikira zimenezo, “basi masiku a zozizwitsa anapita,” ndi zina zotero, monga iwo amachitira. “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu,” kuti mneneri anati zidzakhala mmasiku otsiriza, “koma kumakana Mphamvu yakeyo.”

⁴⁶ Ife tikupeza, mu izi, kuti Iye anali kuwadzudzula iwo, chifukwa iwo anali okakamizidwa kuti ayang’ane pa zizindikiro ndi kukhulupirira zizindikiro. Nowa anawapatsa iwo chizindikiro. Mulungu nthawizonse mu m’badwo uliwonse ankachita ndi munthu kupyolera mu zizindikiro, chifukwa Iye ndi wauzimu. Ndipo pamene pali Mulungu wauzimu, pakuyenera kukhala zinthu zauzimu zikuchitika.

⁴⁷ Ndiye ife tikupeza, mmasiku a Nowa, iwo amene anakhulupirira uthenga wake ndipo analowa mkati, anapulumutsidwa, ndipo iwo amene anakana uthenga wake anawonongeka. Iye anawapatsa iwo chizindikiro cha kumanga chombo.

⁴⁸ Mmasiku a Mose, Mulungu akuyankhula kudzera mmilomo ya munthu amakhoza kuitana ntchentche, utitiri, achule, kutseka miyamba, kumupanga kukhala mwakuda, kudzera mwa mneneri amene anatsimikiziridwa bwinobwino. Iwo amene anakhulupirira natuluka ku Igupto, kudutsa mzere wolekanitsa wa Nyanja Yofiira, anapulumutsidwa. Iwo amene anali mbali inayo, anawonongeka.

⁴⁹ Ndipo Yesu anali kuwauza iwo. Iwo anamutcha Iye, “Bezebule,” kumadzinenera kuti Iye anali kuwerenga malingaliro a anthu. Kapena ena lero, iwo akanakhoza kunena kuti, “Ndi kuwerenga maganizo.” Koma munthu wanzeru aliyense amene amadziwa msempha uliwonse wa kuwerenga maganizo, amadziwa kuti zinthu zimene ife tikuziwona sizingakhale kuwerenga maganizo.

⁵⁰ Tsiku lina, mu Tucson, kunali m’bale wamng’ono wa Baptisti, ndipo iye anapita uko, akumubweretsa Rebekah wanga wamng’ono kunyumba kuchokera ku sukulu, atanyamula mabuku ake. Ndipo iye anapita ku msonkhano. Iye anawaimbira abambo ake, wamishonare uko ku Mexico, mwamuna wabwino, bwanawe wa Billy Graham; ndipo iye anati, “Adadi, fulumirani kunyumba mwamsanga ndithu, ife tawona mphamvu ya Ambuye Yesu ikuwonetseredwa.”

51 Iye anati, “Mwana, vuto lako ndi chiyani?” Anamuimbira iye pa mtunda wautali. Ndipo iye ananena zomwe zinachitika. Iye anati, “Izo zikhoza kuwoneka mu chiwonetsero chotchipa chirichonse.”

52 Ndipo mnyamatayo anakhala pamenepo miniti. Iye anati, “Adadi, ine ndimakukondani inu. Inu mwakhala muli bambo anga, ndipo inu mwayesetsa kundilera ine molondola. Koma ine ndikudabwa ngati ife tingasinthe chosinthira kubwerera ku nthawi imene Yesu waku Nazareti anachita chinthu chomwecho pa magombe a Galileya, ngati mungalolere kuchitcha icho chiwonetsero chotchipa?” Bamboyo anasiya malo ake antchito, ndipo anabwera ndipo anadzakhutitsidwa.

53 Inu mukuona, Yesu anali kuyesetsa kuti awauze iwo, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Ndani wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo, lomwe liri kusakhulupirira? Ngati ine sindinakwaniritse mawu onse amene analembedwa a Ine, ndiye inu mukhoza kuloza chala chanu pa Ine; koma Ine ndachita ndendende basi zimene Lemba linati Ine ndikanati ndidzachte.”

54 Oh, ngati mpingo ukanangotenga maimidwe amenewo, usikuuno, monga womuimira Yesu Khristu, ndi kuti, “Kodi ife taperewera pati? Mulungu, ine ndikufuna kukhala moyo kuti ndidzawone tsiku limene mpingo wa Yesu Khristu ukhoza kukhala mmodzi mu cholinga ndi mtima ndi thupi, utayima mu mphamvu yathunthu yodzozedwa ya Mzimu Woyera, kuti uchite ndi kugwira ntchito monga Yesu Khristu anachitira, ndi Mulungu mwa iwo, aponso.”

55 Tsopano Iye anayamba kubwerera mmbuyo ndi kukawadzudzula iwo. Iwo amadziwa kuti Mulungu, mmibadwo yonse, amatumiza mphatso. Ndipo pamene Mulungu atumiza mphatso ku dziko lapansi, ndipo iyo nkukanidwa, fuko limenelo kapena m’badwo umenewo umapita ku chiweruzo. Ndipo ngati Mulungu atumiza mphatso ndipo iyo nkulandiridwa, m’badwo umenewo ndi wodalitidwa.

56 Ine ndinali kuganiza usikuuno, pamene ine ndimabwera, kuganizira pa izi, kuti, “Chingakhale chiyani ngati Amereka yense, usikuuno, atakhulupirira mphatso ya Mulungu imene ife tailandira?”

57 Yesu pano akunena za nthawi ya—ya Yonasi, kapena Yona kwenikweni ndi chimene icho kwenikweni chiri. Ndipo anthu ambiri amamuweruza Yona, ndipo iwo amanena kuti Yona anali. . . Inu mukuti, “Iye anali Yona. Iye anachita *izi, izo,*” chifukwa Yona, ife timaganiza, anachoka mu chifuniro cha Ambuye.

58 Koma ndiloleni ine ndiyesere kuzilongosola izo, usikuuno. Baibulo linati, “Mapazi a olungama amatsogozedwa ndi

Ambuye.” Nthawizina, Iye amatipangitsa ife kuchita zinthu mosiyana kwambiri ndi zomwe ife timaganiza; koma ife nthawizonse, ngati ife tikutsatira kutsogolera kwa Mzimu, ife nthawizonse timakhala mu chifuniro Chake. Mulungu amachita zimene Iye akufuna. Iye anamuukitsa Farao kwa cholinga chomwecho; ndipo anaitana, anati Iye anamukonda Yakobo ndipo Iye anamuda Esau, iwo asanabadwe nkomwe. Tsopano cholinga cha Mulungu chiyenera kukwaniritsidwa. Kodi wowumba...kapena dongo linganene kwa wowumba, monga tikuzipeza mu Aroma 8 ndi 9.

⁵⁹ Penyani, ife tikupeza apa kuti Yona analamulidwa ndi Mulungu kuti apite kumusi ku Nineva, kuti akalalikire, ndi kukanena kuti mmasiku forte mzinda umenewo udzawonongeka, chifukwa Nineva unali mzinda waukulu wodzadza ndi tchimo, dziko lachikunja. Iwo ankapembedza mafano. Iwo anali, ntchito yawo kwenikweni inali kuwedza, chifukwa iwo amakhala mmphepete mwa nyanja. Ndipo wawo—wokhalamo wawo anali kuti...ntchito, inali usodzi. Ndipo Yona, mmalo motenga chombo...Ndipo mwinamwake chombo sichimatuluka basi pa nthawi imeneyo. Koma iye anatenga chombo wa ku Tarisi. Ndipo ife tikupeza ndi kumvetisa vuto limene Yona analowamo, kunja uko pa nyanja. Ine ndikukhulupirira kuti zonse izo zinadzedwa ndi Mulungu. Nyanja inavutika, ndipo Yona anati, “Mangani manja anga ndipo mundiponyere ine mnyanja.” Ndipo Mulungu anali atakonza nsomba, monga ife timazitchulira “chinsomba,” ndi kuti imumeze mneneriyo.

⁶⁰ Zaka pang’ono zapitazo, ine ndinali mu Louisville, Kentucky, iwo—iwo anali ndi chinsomba pa...mafupa a chimodzi, pa—pa galimoto. Ndipo Ricky wamng’ono uyu atayima pamenepo, ali ndi magalasi ake pa mphuno yake, ndipo amawoneka kuti anali ndi maphunziro ochuluka kuposa momwe iye analiri ndi luntha loti aziziletsa nalo, iye anali kuyesetsa kuti afotokoze za chinsomba ichi. Iye anati, “Inu mukudziwa, nthano yakale ya Baibulo, kuti chinsomba chinamumeza Yona.” Iye anati, “Imeneyo ndi nthano chabe.” Anati, “Chifukwa, inu mukuona, iwe sungakhoze konse kuponyera mpira kuti imeze, iyo inali yaing’ono kwambiri, ndipo iyo siyikanakhoza kumumeza munthu.”

⁶¹ Izo zinali zondikulira kwambiri kuti ine ndingoima. Ine—ine ndinati kwa iye, ine ndinati, “Bwana, ine—ine ndikufuna kukonzani zimenezo.”

Iye anati, “Ndi chiyani chimenecho?”

⁶² Ndipo ine ndinati, “Inu mukuona, iye akhoza...Chinsomba chimenecho mwina sichikanakhoza kumumeza iye, koma Baibulo linanena, kuti, ‘Mulungu anakonza chinsombacho.’ Icho chinali chomangidwa mwapadera. Mulungu anachipanga icho

kukhala chachikulu mokwanira kuti chimumeze iye.” Mukuona? Ine—ine ndinangomverera ine ndikanakhala wopandukira Baibulo ngati ine ndikanapanda kupereka umboni wanga, kusonyeza mangamanga, chifukwa anthu amaima pamenepo akuseka. Ine ndikukuuzani inu, icho chinali chinthu chosiyana pamene icho chinanenedwa, mwaona, icho sichinali choseketsa kwambiri, pamene ine ndinati, “Inu simukuwadziwa Malemba. Lemba linati, ‘Mulungu anakonza chinsomba.’ Iye anapanga ichi kukhala chapadera.”

63 Monga mtsikana wamng’ono nthawi ina, akupita kuchokera ku tchalitchi, anati iye anali wosangalala. Tsitsi lake laling’ono atalipesera kumbuyo, ndipo iye anali ndi nthawi yopambana, akuimba matamando a Mulungu. Wachikunja pa kona anati, “Iwe wakondwa kwambiri chifukwa chiyani, dona wamng’ono?”

Iye anati, “Ine ndapulumsidwa kumene, ndikupita Kumwamba.”

64 Iye anati, “Ndi chiyani chimene iwe uli nacho pansu pa nkono wako, chinthu icho chimene iwo amachitcha Baibulo?”

Iye anati, “Inde, bwana, ndi limenelo.”

Anati, “Iwe sumalikhulupirira limenelo?”

Anati, “Mawu aliwonse a zimenezo.”

65 Anati, “Chabwino, ine ndikuganiza iwe umakhulupirira nkhani ija ya chinsomba ikumumeza Yona?”

66 Iye anati, “Inde, bwana, ine ndimaikhulupirira iyo. Ngati Baibulo likananena kuti Yona anameza chinsombacho, ine ndikanakhulupirira zimenezo.”

67 Ndipo iye anati, “Tsopano iwe ungatsimikizire motani kuti—kuti chinsomba chinamumeza Yona, mwanjira ina iliyonse kupatula mwa chikhulupiriro?”

Iye anati, “Pamene ine ndidzafika Kumwamba, ine ndikamufunsa Yona.”

Iye anati, “Ndiye nanga bwanji ngati Yona sali kumeneko?”

68 Anati, “Ndiye inuyo mukamufunsa iye.” Kotero izo zinangopita kukasonyeza zomwe ziti zidzachitike, iye anapita mbali inayo. Ndipo izo zikufotokoza izo.

69 Koma ine ndikukhulupirira kuti chinsomba chinamumeza Yona. Tsopano, ndi manja omangidwa, mmimba mwa chinsomba, kutali komwe pa nyanja, pafupifupi kuya kwa utali miyezo forte.

70 Tsopano akazi inu mukudziwa, ndi nsomba zanu zazing’ono zagolide. Nsomba imayenda m’madzi kuti ipeze chakudya chake. Ndipo iyo itatha kupeza chakudya chake, iyo imadzazitsa mimba yake yaing’ono, iyo imapita pansu pa mbaleyo ndikukapumitsa chosambira chake chaching’ono pamenepo. Mwaona, iyo

ikupuma. Zosambirira zake zimaigwira iyo. Ndipo tsopano iyo imamasuka chifukwa iyo yatopa ndi kuyendayenda.

⁷¹ Tiyeni tiganizire nsomba yaikulu iyi inachita chinthu chomwecho. Pamene iyo inamumeza mneneri, iyo inatsikira pansi, kulemera kwake kwakukulu kwa matani ambiri, inakagona pansi pamenepo tsopano, ndi mneneri mmimba yake. Ndipo mneneriyo anali akadali wamoyo. Iyo inamumeza iye. Ndipo Yona ayenera kuti anatembenuzika, pansi mmimba mwa chinsombachi. Ndipo, inu mukudziwa, kulikonse kumene iye amayang'ana, iye amakhoza kuwona mimba ya chinsomba.

⁷² Ndipo ine kawirikawiri ndakhala ndikuganizira za anthu, kumati, "Ine ndinapemphereredwa usiku wathawu, koma dzanja langa si labwinoko. Ine ndinapemphereredwa, ndipo ine sindikumverera bwinoko mulimonse." Chabwino, inu mukuyang'ana pa zizindikiro, pamene inu mukuyang'ana pa zimenezo. Ngati abusa anu anakupemphererani inu, anakudzozani inu ndi mafuta, kapena kachitidwe kalikonse kamene iye amagwiritsa ntchito Baibulo la Mulungu, inu muyenera kukhulupirira izo. Inu muyenera kuzikhulupirira izo.

⁷³ Tsopano ine sindikuganiza kuti aliyense wa ife anayamba wakhalapo ndi zizindikiro zochuluka monga Yona anali nazo, pakuti, mbali iliyonse imene iye ankayang'anira, iyo inali mmimba ya chinsomba. Koma inu mukudziwa zimene iye ananena? Iye anati, "Izo ndi zakutha." Iye sanazikhulupirire izo. Iye anati, "Kamodzinso Ine ndidzayang'ana ku kachisi Wanu woyera."

⁷⁴ Tsopano Yona ankadziwa kuti pamene Solomoni ankampereka kachisi, Mulungu anatsimikizira Kukhalapo Kwake pa kachisi, pakulowa monga Lawi la mtambo, ndipo analowa mkati ndipo anapita kuseri kwa Malo Oyera, pa Mpando Wachifundo ndi pamwamba pa chombo, ndipo anadzakhala pansi. Ndipo Solomoni anapemphera, "Ambuye, ngati anthu Anu adzakhale mu vuto, kulikonseko, ndipo akadzayang'ana ku malo oyera awa, ndi kupemphera, ndiye Inu mudzawamve iwo kuchokera Kumwamba."

⁷⁵ Tsopano, ngati Yona, pansi pa zochitika zimenezo, akanakhoza kukhala ndi chikhulupiroro mu pemphero la munthu, munthu, yemwe kenako anabwerera mmbuyo; ndi pa kachisi amene amangidwa ndi manja a munthu, amene Mulungu anadalowamo; ndipo anawomboledwa kwa zoterozo, zizindikiro monga zimenezo; ndi mochuluka bwanji tiyenera ife, usikuuno, pansi pa chochitika chathu chaching'onochi, pakati pomwe pa Kukhalapo kwa Mulungu wamkulu Mwiniwake, kumene ife tikuwawona anthu akuchiritsidwa, akupulumutsidwa, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera! Musayang'ane ku kachisi wachibadwa; koma muziyang'ana ku kachisi Kumwamba, kumene Khristu akukhala pa dzanja

lamanja la Ufumu, ndi mphamvu, ndi Magazi Ake Omwe, kuti apange kupembedzera pa kuvomereza kwathu. Iye tiyenera kumachita manyazi ndi kufooka kwathu. Tsopano, mpaka inu mutakhala ndi chikhulupiriro chabwinoko kuposa chimene Yona anali nacho, musamamutsutse iye.

⁷⁶ Zindikirani, ndiye ife tikupeza kuti Mulungu, pansu pa pemphero limenelo ndi chikhulupiriro chimenecho... Iye akanakhoza kuika hema wa mpweya kumeneko; ine sindikudziwa chimene Iye anachita. Koma iye anakhala, molingana ndi Mawu Omwe a Khristu, masiku atatu ndi usiku mmimba mwa chinsomba chimenecho. Ndiyeno tiyeni tiganizire za zimenezo, pafupifupi, zikhoza kukhala pafupifupi leveni koloko masana, asodzi onse anali pafupifupi atakonzeka kuti alowe ku chakudya chawo cha masana, ndipo iwo anali pafupi kutenga maukonde awo. Ndipo achikunja awa ankapembedza zinyama, ndipo mulungu wa mnyanja anali chinsomba. Ndipo basi pafupifupi pakati pa tsiku, apa panabwera mulungu wa mnyanja akubwera pamenepo, chinsomba, anatulutsa lirime lake, ndipo mneneriyo anatuluka kuchokera mkamwa mwake. Nzosadabwitsa iwo analapa, ndithudi, chifukwa mulungu anamulavula mneneri. Ndipo iye anapita kudutsa misewu, akuti, “Mmasiku forte malo awa adzawonongedwa.” Mwaona, Mulungu amadziwa momwe angachitire zinthu.

⁷⁷ Tsopano, iwo anamufunsa Yesu chizindikiro, ndipo Iye anawauza iwo kuti, “M—m’badwo woyipa ndi wachigololo umafunafuna zizindikiro.” Ndipo, tsopano, ine ndikudziwa pali kutanthauzira kumene Iye anali kuwathawuza iwo. Izo nzoona. Koma ine ndingopitiriza izo, kukhala ndi tanthauzo lapawiri.

⁷⁸ Ndi liti pamene ife tinayamba takhalapo ndi m’badwo woyipa ndi wachigololo wochuluka kuposa umene ife tiri nawo pakali pano? M’badwo woyipa ndi wachigololo! Iwo adzanena kwa iwe, pita uko pa msewu, ndikukati, “Kodi ndiwe mchiritsi Wauzimu?”

“Ayi. Khristu ali.”

⁷⁹ “Chabwino, ngati ndiwe mchiritsi, kapena iwe umakhulupirira, iwe umati ndiwe mchiritsi; ine ndikudziwa munthu ali kumusi kuno akudwala, bwera udzamuchiritse iye. Ine ndikudziwa iwe umati unaukutsa akufa; munthu anafa ndipo iwe unamuukitsa iye? Ife tiri nawo manda odzadza ndi iwo kumusi kuno; utadzatsimikizira izo kwa ife.”

⁸⁰ Kumbukirani, ameneyo ndi mdierekezi wakale yemwe uja amene anati, “Ngati Inu muli Mwana wa Mulungu, lamulirani miyala iyi ikhale mkate.”

⁸¹ Ndi mdierekezi wakale yemwe uja yemwe anaika chisanza pa maso a Ambuye wathu, mnyumba yachifumu mmawa umenewo, anaphimba maso Ake, ndipo iwo anatenga ndodo,

asilikali oledzera amenewo, okangana, ndipo anadzamumenya Iye pa mutu ndi iyo, ndiyeno nkupatsirana ndodoyo, wina kwa mzake, ndipo anati, “Ife tamvetsedwa kuti Inu mumadziwa zinsinsi za mu mtima. Ife tamvetsedwa kuti Ndinu mneneri. Ngati Ndinu mneneri, loserani ndipo mutiuze ife yemwe wakumenyani Inu. Ife tikhulupirira zimenezo ndiye.” Mwaona, ameneyo ndi mdierekezi wakale yemwe uja. Mukuona? Mulungu sachitira chisudzo aliyense.

⁸² Ndi mdierekezi wakale yemwe uja yemwe anati, “Tsika pa mtandapo. Tiyeni tikuwoneni Inu mukuchita chozizwitsa.” Mdierekezi ameneyo ali moyo lero.

⁸³ Ndipo Yesu ananena, kuti, “M’badwo woyipa, wofooka, wachigololo udzafunafuna chizindikiro, ndipo iwo adzachepeza icho. Pakuti monga Yona anali mmimba mwa chinsomba, kwa masiku atatu ndi usiku utatu, chomwechonso Mwana wa munthu adzakhala mu mtima wa dziko lapansi.” Ndiye ndi mtundu wanji wa chizindikiro umene Iye anali kuwukamba? Chizindikiro cha chiwukitsiro. Ndipo zitatha zaka thuu sauzande za kulalikira Uthenga, zaka thuu sauzande za kutsutsa, Baibulo lakwera kudutsa zonsezo. Ndipo, usikuuno, Yesu Khristu ali pakati pathu, mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake, akuchita zinthu zomwezo zimene Iye ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Uno ndi m’badwo wofooka uja ndi wachigololo.

⁸⁴ Yohane Woyera 14:12, Yesu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso azidzazichita.” Mukuona? “Komabe kanthawi pang’ono ndipo dziko, dongosolo la mdziko, silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine. Ameneyo ndi wosakhulupirira, dziko, dongosolo la mdziko, dongosolo la mpingo, silidzandiwonanso Ine. Komabe inu mudzandiwona Ine, wokhulupirira, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezere a dziko lapansi.”

⁸⁵ Ndipo m’badwo woipa ndi wachigololo uno umene ife tiri nawo pa dziko lapansi, wa kuwasereula Mawu apachiyambi a Mulungu, kumapanga zoseleula a—za mpingo, ukulandira usikuuno chizindikiro cha chiwukitsiro. Chifukwa, zinthu zimene Yesu Khristu akuchita lero, mu mpingo, palibe munthu mdziko lapansi angakhoze kuchita izo kunja kwa Yesu Khristu. Ndipo icho ndi chizindikiro kuti Iye ali moyo usikuuno. Iye anauka kwa akufa, zaka thuu sauzande zapitazo, ndipo ali basi wamoyo usikuuno monga Iye anali pamene Iye ankayenda mu Galileya. Amen. Chizindikiro cha chiwukitsiro!

⁸⁶ Ndiye ife tikuzindikira, mpaka mmusi, Iye amakamba za nthawi ya Solomoni. Iye anati, “Amuna aku Nineva analapa pa kulalikira kwa Yona, ndipo alipo wamkulu kuposa Yona pano.” Iye anati, “Ndipo monga mmasiku a Solomoni, momwe mfumukazi ya Kummwera inabwera kuchokera ku madera

akutali a dziko lapansi, kuti idzamve nzeru za Solomoni, ndipo wamkulu kuposa Solomoni ali pano.”

⁸⁷ Mwaona, iwo sanakhoze kuzimvetsa zimenezo. Iwo anali ochedwa kumvetsa. Yesaya anati, “Iwo ali nawo maso ndipo osatha kuwona, makutu ndipo osatha kumva.”

⁸⁸ Ine ndinena izi ndi chikondi. Pentekoste, pafupifupi ikufika mwanjira yomweyo. Chinthu chimene Mulungu analonjeza, chimatidutsa pomwe apa pa ife, ndipo ife timangozisiya izo zizipita. Chimene chawavuta anthu Achipentekoste, ndi ichi, iwo awona zochuluka kwambiri za Mulungu . . .

⁸⁹ Izo zikundikumbutsa ine za mwambi wakale, kapena nkhani yomwe ine ndinawerenga kamodzi ya mlembi yemwe analemba za nyanja, ndipo iye anati iye anali asanaiwonepo iyo. Monga ife tinamva kuti Stephen Foster, wolemba wokonedwa ndi anthu, analemba za “Swanee” Mtsinje, ndipo anali asanawonepo Mtsinje wa Suwannee. Ndipo wolemba uyu anali atalemba za nyanja, ndipo anali asanaiwonepo nyanja. Nthawi ina iye anatenga ulendo wopita ku nyanja. Ndipo ali panjira yake iye anakumana ndi woyendetsa panyanja wachikulire, wojaira wakale, akubwera, ali ndi ndevu za imvi pa nkhope yake, ndi chisononkho chake cha chimanga mkamwa mwake. Iye anati, “Iwe ukupita kuti, munthu wanga wabwino?”

⁹⁰ Iye anati, “Ine ndikupita ku nyanja.” Iye anati, “Ndine—ndine wandakatulo.” Iye anati, “Ine—ine ndikungofuna kukaiwona iyo. Ine ndikufuna ndikawone mafunde ake oyera pamene mafunde amphelo akuwomba pa buluu. Ine ndikufuna ndikawone kunyezimira kwa mlengalenga mmadzi a buluu, kununkhiza mchere mu mlengalenga. Ine ndikufuna kuti ndikamve akatawa pamene iwo akufuula ndi kukuwa, pamene iwo akupita mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa pamadzi.”

⁹¹ Wojaira wakaleyo anatenga chisononkho chake cha chimanga kuchokera pakamwa pake, ndi kudzalavula. Iye anati, “Ine ndinabadwira kumeneko, zaka sikisite zapitazo. Ine sindimawona chirichonse chosangalatsa cha iyo.” Bwanji? Iye anali atawona zochuluka kwambiri za iyo, iyo inakhala yawamba kwa iye.

⁹² Ndipo ndiro limene liri vuto ndi inu Achipentekoste. Inu mwaona zochuluka kwambiri za matamando ndi madalitso a Mulungu, mpaka izo zikutelera kudutsa mwa inu. Ife tiyenera kukhala aulemu ndi zinthu izi, ndi kulemekeza chirichonse chimene Mulungu akupereka kwa ife.

⁹³ Tsopano, masiku a Solomoni, monga wazafioloje aliyense, munthu wa Mwamalemba akudziwa kuti uwo unali m’badwo wa golide wa Ahebri. Iwo analibe nkondo. Iwo, iwo unali pafupifupi ngati Zakachikwi kwa iwo. Tsiku lalikululu! Iwo anamanga kachisi. Mafuko onse ankawawopa iwo. Iwo ankachita mantha kuti achite chirichonse, chifukwa iwo

amadziwa kuti anthu anali ndi mtima umodzi ndi mgwirizano umodzi. Mulungu anawapatsa iwo mphatso, ndipo iwo anayikhulupirira iyo. Iwo anayivomereza iyo, ndipo ndi mtima umodzi ndi mgwirizano umodzi iwo amagwira ntchito ndi iyo.

⁹⁴ Oh, ngati ife, anthu aku Amerika angakhoze, usikuuno, a Apresbateria onse, ndi Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi Achipentekoste, mungaphwasule mwambo wanu umene chipembedzo chanu chamanga pozungulira inu, kulekanitsa ubale, “mwakuwoneka osakhala nacho chikhulupiriro.” Ngati ife tingakhoze kuchoka mu chigoba chakale icho chimene ife tirimo, ndipo nkukhoza kubwera pamodzi ndi kudzalandira mphatso ya Mulungu, pa maziko amene Iye anayiperekerera iyo kwa ife, icho chingakhale chobisalirapo bomba chabwino chimene ine ndikuchidziwa. Ine kulibwino ndiyime kuseri kwa iyo, malonjezo a Mulungu, kuposa zobisalirapo mabomba zonse zimene iwo akanakhoza kumanga. Motani, fuko lotani, ndi chitsitsimutso chotani chimene chiti chidzakhale, momwe mafuko ena angamawopere kuchita chirichonse za iyo. Mulungu watipatsa ife mphatso, koma ife timaipeputsa iyo.

⁹⁵ Ife timayesera kuyibweretsa iyo mu gulu limodzi laling’ono, ndi kumati, “Ife tiri nayo iyo, ndipo inu mulibe kanthu kalikonse kochita nayo iyo, chifukwa inu simukuwona kupyolera mmagalasi anga.” Ife sitikuyenera kumachita zimenezoyi. Izo si zolondola. Bola ngati mdierekezi akakupangitsani inu kuti muzimenyana wina ndi mzake, iye samasowa kuti azimanya.

⁹⁶ Koma pamene inu muwona kulumikizana kumeneko kwa mphamvu za Mulungu, akusonkhanitsa mpingo Wake pamodzi kuchokera ku mphepo zinayi za dziko lapansi, ndiye inu muwona chinachake chikuchitika.

⁹⁷ Ife tikupeza kuti, mmasiku a Solomoni, Mulungu anamupatsa iye mphatso ya kuzindikira za mumtima. Iyo inali mphatso yaikulu, mphatso yozindikira maganizo, ndi zina zotero, ya nzeru. Ndipo anthu anazungulira pa iyo. Iwo anamupanga iye mfumu. Ndipo, inu mukudziwa, iye anadzakhala choyankhula cha dziko lapansi. Aliyense ankayankhula za Israeli. Tsopano, iwo analibe matelefoni ndi matelevizioni, ndi zinthu, ndiye, iwo ankanyamula nkhani kuchokera pa mulomo kupita ku khutu. Ndipo anthu aliwonse amene ankabwera amadzawona mphatso yaikulu iyi ya Mulungu, ikugwira ntchito, ndipo anthu amakhoza, bwanji, iwo—iwo amakhoza kumuuzza aliyense. Ndipo kutchuka kwake kunapita padziko lonse. Ndipo onse a iwo analibe nkondo, analibe vuto, chifukwa iwo analandira mphatso imene Mulungu anawapatsa iwo.

⁹⁸ Ife tonse, usikuuno, ife Apresbateria, Amethodisti, Abaptisti, chigawo cha Chipentekoste, tonse titakhoza kungotaya malingaliro athu, ndi kubwerera ndi kudzawona

zomwe Mulungu ananena za Iwo, ndi momwe Iye ananenera kuti Iwo uyenera kuperekedwa. Iye sangakhoze kuwusinthwa Iwo. Momwe Iwo unagwera pa Tsiku la Pentekoste, ndi momwe Iwo unagwera ku nyumba ya Kornelio. Ndipo nthawi iliyonse imene Iwo unayamba wagwapo, Iwo umagwa mwanjira yomweyo, pansu pa dongosolo lomwelo limene Petro analemba, mu Machitidwe. Ndipo umu ndi mmene izo zikuimira. Izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo. Njira ina iliyonse... Palibepo malo ena mu Baibulo kumene iwo anayamba awulandira Iwo mwanjira ina iliyonse kupatula kutsatira dongosolo lake la Machitidwe 2. Ndizo ndendende. Ndizo, ndipo ife tiri nawo Iwo lero, ndi momwe iwo uyenera kubwerera.

⁹⁹ Koma moonamtima, munthu amamulandira Mulungu ndi kumukhulupirira Iye, koma ngati iwo akanati basi... Ndiye iwo amadzichotsako okha, ndipo, “Kuti, ife tiri nazo *izi* ndipo ndizo zonse zomwe ziripo kwa Iwo.” Ndiye iwo amadzilekanitsa okha. Ndiye iwo samatenga vumbulutso latsopano ayi. Iwo amalipanga ilo bungwe. “Izi ndi izo. Ichi ndi chiphunzitso chathu,” kuthera ndi a—mpumiro. Ngati inu mukanakhala ndi chipembedzo chimene chikanatsirizitsa chiphunzitso chanu ndi koma, “Ife timakhulupirira *izi*, kuwonjezera zochuluka zonga zomwe Mulungu angatiwonetsere ife,” ndiye izo ziri bwino, ine ndingatsatire chimenecho; koma osati ndi mpumiro. Chifukwa, Mulungu ndi Mulungu, ndipo nthawi ikusunthabe.

¹⁰⁰ Ife nthawizonse tikumayesetsa kumayang’ana mmbuyo ndi kumawona zimene Moody ananena, zimene Sankey ananena, zimene Finney ananena, zimene Wesley ananena, zimene Luther ananena. Iwo anali anthu a tsiku limenelo.

¹⁰¹ Sayansi siimayang’ana mmbuyo ndi kuwona zimene sayansi inanena. Bwanji, zaka firii handiredi zapitazo, wa sayansi wachi Frenchi anatsimikizira kuti ngati munthu angapite pa liwiro lowopsya la mailosi sarte pa ora, mphamvu yokokera pansu ikhoza kumuchotsa iye pa dziko lapansi. Kodi inu mungalingalire sayansi yamakono ikunena zimenezo? Lero iye akumathamanga pafupifupi mamailosi thuu sauzande pa ora, kuyesetsa kuti apezze chinachake choti chisasungunule chitsulo kotero kuti iye azikhoza kuyenda mailosi foro sauzande pa ora. Iwo samayang’ana mmbuyo ndi kulozera kwa iye. Iwo amayang’ana chitsogolo.

¹⁰² Koma mpingo nthawizonse umayang’ana mmbuyo. Tiyeni tiyang’ane mmwamba! Pakuti, mphamvu zawo ziri zoperewera. Ndipo ife tiri ndi mphamvu zopanda malire, “Pakuti zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira mwa Mulungu.” Chikhulupiriro chenicheni chimavomereza Mawu aliwonse amene Mulungu wapereka, ndi “ameni.” Osati, “Chabwino, izo zinali za m’badwo wina.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!

¹⁰³ Tsopano ife tikupeza kuti Solomoni, nkhani inafalikira kwambiri mpaka iyo inapita njira yonse mpaka ku Sheba. Ndipo iwo anali ndi mfumukazi kumusi uko, iye ayenera kuti anali dona wamng'ono wabwino. Iye amakhoza kuwayendetsa anthu ake. Ndipo, inu mukudziwa, iwo anayamba kumuza iye kuti kunali a—Mulungu wamkulu mu Israeli, ndipo Iye anali atadzozza munthu wokhala ndi mphatso ya kuzindikira za mumtima yemwe anali munthu wapamwamba, kuti palibe munthu akanakhoza kukhala ndi nzeru monga choncho. Izo zinkayenera kuchokera kwa mulungu. Ndipo, inu mukudziwa, “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva Mawu.” Ndipo izo zinakhudza mtima wake, monga izo zinachitira ndi mkazi wamng'ono wopanda khalidwe pa chitsime usiku wathawu. Izo zinakhudza mtima wake, ndipo iye anayamba kukhumba kuti apeze za zimenezi.

¹⁰⁴ Ine ndikuganiza izo zikumukakamiza aliyense wa ife, pamene ife tipeza pamene Moyo Wamuyaya unayikidwapo, chifukwa ife tikuyesetsa kuti tikhale moyo.

¹⁰⁵ Chabwino, wapaulendo aliyense amene ankadutsa, iye mwinamwake ankaima ndi kuwabweretsa iwo ku nyumba yachifumu. “Kodi inu munadutsa mu Palestina?”

¹⁰⁶ “Inde, ife tiri ndi zodzola zina, ndi ngale zina ndi zinthu zochokera kumeneko.”

“Chabwino, kodi izo nzoona za mphatso yaikulu ija ya Mulungu wawo?”

¹⁰⁷ “Izo ndi zooni. Ine ndinayiwona iyo ikugwira ntchito.” Mwaona, chikhulupiriro chimadza pakumva.

¹⁰⁸ Ndiyeno iye anayamba ku, kuyamba kuchita ludzu. Iye ankafuna kuti ayiwone iyo, iyemwini.

¹⁰⁹ Tsopano iye anali ndi zovuta zambiri zoti adutsemo. Chinthu choyambirira, iye anali wachikunja. Chinthu china, iye anali mfumukazi. Ndipo sindikukaika, kuti achite izi, iye ankayenera kuti apite kwa wansembe wake yemwe, kuti akatenge chilolezo choti apite kuti apite kuti akamve izi. Chotero ine ndikukhoza kulingalira... Ngati ine ndikumveka mosinjirira, ine sindikutanthauza izi tsopano. Ine ndingopereka seweru pang'ono apa. Ine ndikukhoza kulingalira iye akupita kwa wansembe, ndi kumati, “Atate woyera?”

“Inde, mwana wanga wamkazi,” anatero wansembe.

¹¹⁰ “Ine ndakhala ndikumva nkhani kuti uko mu Israeli iwo ali naye Mulungu kumeneko, amene ndi munthu wodzozedwa ndi kuzindikira za mumtima Kwake Komwe ndi mphamvu.”

¹¹¹ “Tsopano tamvetsera, mwana wamkazi. Ngati, ngati milungu yaikulu ingasunthe konse, iyo ingasunthe pakati pathu.” Inu mukudziwa, iwo samasowa kuti onse akhale ansembe achikunja, kuti akhulupirire zimenezo. Mukuona?

“Ngati iyo ikanati isunthe konse, iyo ingachite chirichonse mu bungwe lathu. Iyo siyingakhale pakati pa ena amenewo, wawona. Kuwonjezera apo, iwo ndi gulu la oyera-odzigidubuzo.” Chabwino, ine sindimafuna kuti ndinene zimenezo, mwaona, koma inu mukudziwa. “Iwo—iwo—iwo, iwo alibe zochulukwa kwambiri. Ilo langokhala gulu chabe la otentheka. Iwo amanena mitundu yonse ya nkhani zokhudza kuwoloka Nyanja Yofiira, chimene si china koma nthano. Koteri iwe sangakhoze kukhulupirira gulu ilo kuntunda kumeneko, chifukwa iwo ndi—iwo angokhala gulu chabe la osadalirika. Tsopano ngati pali mphamvu iliyonse, iyo ili mwa mulungu wamkulu, Dagoni, kapena ena a awa pano.”

¹¹² Ine ndikukhoza kumumva mkazi wamng’onyo, akuyankhula miniti, iye anati, “Koma, inu mukudziwa, iwo akumandiuza ine kuti Mulungu uyu amene iwo ali naye ndi Mulungu weniweni.”

“Bwanji,” iye anati, “mwana wamkazi, *ameneyo* ndi mulungu weniweni.”

“Koma, iwo, iwo akumandiuza ine kuti Mulungu uyu kuntunda uko ali nawo moyo.”

¹¹³ Mwaona, pamene—pamene—pamene chinachake chikugwira kwenikweni pa mtima, Mulungu adzayankhula nawe ngati utamangopitiriza kuyankhula. Mwaona, “Musaganizire zomwe muti mukayankhule; izo zidzaperekedwa kwa inu mu ora limenelo.”

¹¹⁴ Ndiye anati, “Iwo akumanena kuti Mulungu uyu kuntunda kuno ndi Mulungu amene amawakonda anthu Ake, ndiye Iye amabwera kumeneko ndipo Iye amadzizindikiritisa Yekha kupyolera mwa anthu Ake.”

“Ah, palibe kanthu kwa izo. Mvetsera.”

Oh, inu mukuti chiyani? “Tsopano miniti yokha. Ine ndikupita kumeneko.”

¹¹⁵ “Ngati iwe utapite kumeneko, iwe, bwanji, iwe udzabweretsa chamanyazi. Iwe usakakhale nawo pa chitsitsimutso chimenecho. Chifukwa, ife sitimagwirizana nawo, iwe ukudziwa, koteri iwe usakachite zimenezo.” Ukuona?

¹¹⁶ “Ndipo inu mukudziwa,” iye anati, iye anati, “agogo-agogo anga aakazi ankatumikira fano limenelo, chosedmedwa chimenecho, kapena agogo anga aakazi ndi amayi anga, anthu anga onse ankatumikira mafano amenewo, ndipo palibe mmodzi wa iwo yemwe anandisonyezapo chidutswa chimodzi cha moyo. Iwo ali basi. . . Ine sindikusamala kuchulukwa kwa mipukutu yomwe iwe ungakhoze kuwerenga, ndi zinazonse, iwo sanasonyeze chidutswa chimodzi cha moyo. Ndipo iwo akuti, ‘Uwu ndi Moyo.’ Ndipo uwu ndi. . . Ine zikundikhudza zimenezo.”

117 Chabwino, ine ndikukhoza kumumva iye akuti, “Tsopano, taonani, ngati utapite kumeneko, ine ndiyenera kuti ndidzakuchotse iwe. Ine ndidzatenga zako. . . Ndiwe membala wokhazikika kuno, iwe ukudziwa. Ndipo ngati ine. . . Ndipo iwe uli ndi ulemu wina, ndipo iwe udzazitsitsa kutchuka kwako ngati udzapite pakati pa gulu ngati limenelo.” Ukuwona?

“Chabwino, mulole izo zikhale kutchuka, kapena ayi!”

118 Inu mukudziwa, pamene Mulungu agwira pa mtima wa winawake, palibe chimene chiti chidzaima mu njira yawo. Iwo akafika kumeneko, mulimonse, ndipo Mulungu adzasamalitsa zimenezo; ine sindikusamala ngati ali mwamuna, mkazi, mwana, mlaliki, m’busa, aliyense yemwe ali, pamene njala ibwera yofuna Mulungu.

119 Tsopano ife tikumupeza dona wamng’ono, pamene iye anakonzeka, iye anati, “Chabwino, ine—ine ndikupita, mulimonse.”

120 “Koma ife tikuchotsa iwe. Dzina lako silidzakhala apa.”

“Chabwino, inu mukhoza ngakhale kungolichotsa ilo, chifukwa ine ndikupita.”

121 Chotero tsopano ndiye, iye ankayenera kulipira mtengo. Chotero ambiri a ife sitimafuna kulipira mtengo. Ife kulibwino twigwiritsitse ku kachikhulupiriro kena.

122 Tsopano, mkaziyo sindikukaikira anali ataphunzira mipukutu ya chipembedzo ichi. Iye anali atawona kuti icho chinali chikhalidwe cha Mulungu; ndipo kuti Mulungu, nzeru zonse za Mulungu, zinaperekedwa mphatso kwa munthu, kuti Mulungu Mwiniwake anali akudzifotokoza Yekha, osati kudzera mu fano lina losayankhula, koma kudzera mwa munthu.

123 Momwe kuti chikunja ndi choyimira changwiro, kapena, chotsutsa-. . .kapena, choyimira cha Chikhristu, momwe kuti wopembedza wachikunja amagwada pamaso pa fano ndi kudzilambatitsa yekha, mwanjira imeneyo, kuti iye—iye amakhulupirira kuti fano limenelo likuyankhula moyankha kwa iye.

124 Monga a—a—a Navaho Indian. Iwo anali ndi kamba kwa mulungu wa mvula, ali ndi matope pa nsana wake, ndipo iwo anapanga chimenecho kukhala fano. Ndikupanga chigoba chopanda kanthu, ndipo iwo amakhoza kumaitanira, ndipo amakhoza kumamva liwu lawo lomwe likuphokosera, ndipo iwo ankaganiza kuti ameneyo anali mulungu wa mvula akuyankha kwa iwo.

125 Ndi zosiyana bwanji ndi Chikhristu, ngakhalebe. Ife timadzilambatitsa tokha pamaso pa Mulungu wauzimu yemwe siali fano, ndipo ife timadzazidwa ndi Iye ndipo timadzakhala fano Lake, chifanizo Chake chamoyo cha Iye, tikugwira ntchito, kumayenda pa dziko lapansi ngati choyimira chamoyo cha

Mulungu yemwe ife tikumutumikira. Mulungu mwa munthu! Ndi zosiyana ndi chikunja; iwo anagwa pamaso pa Maria kapena Yosefe, kapena woyera wina, kapena chinachake chonga izo, omwe anafa kwa zaka. Ndipo, koma, inu mukuona, Mzimu Woyera umabwera mu umunthu wamoyo, osati mu fano lakufa; koma kulowa mu chamoyo, ndi kumagwira ntchito kupyolera mwa chamoyo chimenecho, osati kupyolera mu fano. “Inu ndinu akachisi a Mulungu.” Mukuona?

¹²⁶ Chotero ife tikuwona kuti Mulungu samsintha, Iye akuchita chinthu chomwe chomwecho usikuuno monga Iye ankachitira mmasiku a Solomoni. Iye anamupatsa Solomoni mphatso iyi.

¹²⁷ Ndipo ife tikupeza kuti, tsopano mkazi wamng’ono ayenera kuti akonzekere. Tsopano, iye anali ndi zinthu zambiri zoti akumane nazo. Iye anali ndi zochitika zambiri ndi zolepheretsa zochuluka, koma osati chikhulupiriro chake. Chikhulupiriro chake chinalibe chirichonse.

¹²⁸ Tsopano iye ankaganiza izi, “Ine ndikupita kuntunda kumeneko. Ndipo ngati ine ndikupita, ndipo ngati chinthucho chiri cholondola, ine ndikachithandizira icho. Ngati icho sichiri cholondola, ine ndikhoza kubweretsa mphatso zanga pobwerera kunyumba.”

¹²⁹ Inu mukudziwa, iye ayenera kuyankhula ndi anthu ena Achipentekoste. Uko nkulondola. Uh-huh. Uko nkulondola. Kupita kunja kuno ndi kudzitcha nokha Achipentekoste, ndi kumathandizira maprogramu a pa wailesi omwe amaseleula chinthu chimene inu mumachikhulupirira? Ndipo icho ndi cha pakati pa anthu anu omwe, kuti chithandizire dongosolo la Mulungu. Mukuona?

¹³⁰ Tsopano, koma iye anatenga ndalama, golide ndi lubano, ndi zina zotero, ndipo iye ananyamulitsa ngamira zina.

¹³¹ Tsopano, chinthu china, iye anali ndi—ndi ulendo wowopsya. Kumbukirani, ana a Ishmaeli anali mu chipululu, ndipo iwo anali achifwamba. Ndipo zinali zophweka bwanji kwa gulu ilo la achifwamba kuti ligwere pa mfumukazi yaing’ono iyi, ali ndi adindo apang’ono paulendowo ngati olondera, ndi kuwapha iwo ndi kutenga chuma chonse ichi.

¹³² Koma, inu mukudziwa, pamene iwe uli ndi njala ndi ludzu la Mulungu, iwe sumawona chowopsya chirichonse, iwe sumawona kalikonse. Iwe ukuyesetsa kuti ufike kwa Mulungu, ndipo Mulungu nthawizonse amawonetsetsa kuti iwe wakafikako kumeneko.

¹³³ Iye ankafuna kuti akafike kumeneko. Ndicho chokhumba cha mtima wake, chotero Mulungu anali woti awonetsetse kuti iye wakafika kumeneko. Tsopano, iye sanaganizire za chowopsyacho.

134 Iwe sumaganizira za chowopsyacho. Inu sumaganizira za kutsutsidwa. Iwe sumasamala chimene winawake akunena. Ngati mtima wako uli ndi njala kwambiri yofuna Mulungu, cholinga chokhacho chimene iwe uli nacho ndi kufika kwa Iye. Sizimapanga kusiyana kulikonse momwe iwe uyenera kukafikira kumeneko. Kungofika kumeneko! Tsopano, iye anali ndi cholinga chomwecho.

135 Ndipo tsopano, sindikukaikira, iye anapeza mipukutu yonse ndipo anali akuwerenga, pamene iye anali akupitirira. Iwo ayenera kuti ankayenda usiku, chifukwa, Chipululu cha Sahara chija, kuwala kolunjika uko kwa kutentha kumakhala kochuluka, kotentha kwambiri.

136 Tsopano tangoganizani, iye anali ndi mtunda wautali bwanji umene iye ankayenera kuti apite, kuti akawone nzeru ya Solomoni. Ngati mutawuyeza iwo pa mapu anu, ndi mtunda wautali kumusi uko, pafupifupi mailosi firii handiredi. Ndipo inu mukudziwa utali womwe unamutengera iye? Tsopano, iye sanapite mu Cadillac yokhala ndi choziziritsira mpweya, koma iye anapita pa nsana pa ngamira. Ndipo izo zinamutengera iye masiku nainte, miyezi itatu, kuti akafike kumeneko.

137 Nzosadabwitsa Yesu anati, “Iye adzaima ndi m’badwo uno ndi kudzawutsutsa iwo.” Ena a anthu amakhala kutsidya kwa msewu, sadzadetsa nkomwe chitseko kumene chinthu chomwecho chikuchitika. Uko nkulondola. Amen. Nzosadabwitsa kuti iye adzaima mu Chiweruzo ndi m’badwo uno, ndi kudzawutsutsa iwo. Ayi, pamene ife tiri ndi ma Cadillac okhala ndi choziziritsa mpweya, ndi sitima ndi ndege, ndi njira iliyonse, Mulungu anangoziyika izo mmanja mwanu momwe ndipo komabe ife sitikuchita izo. Ndipo iye anabwera mtunda wonse uja kuti adzamve nzeru za Solomoni, ndipo wamkulu kuposa Solomoni ali pano, Ambuye Mulungu Mwiniwake! Zindikirani!

138 Ndiye ife tikupeza kuti iye anayamba kudutsa mchipululu, akuwerenga mipukutu imeneyo, potsiriza iye anakanikizabe mpaka iye anakafika kumeneko.

139 Mwinamwake anafika kumaloko, bwalo la nyumba yachifumu kapena kulikonse kumene kunali, ndipo anamanga mahema ake, chimene chinali chachizolowezi mmasiku amenewo, ndi ana aakazi ake aang’ono ndi adindo ake, anamanga.

140 Ndiyeno tiyeni tingoganiza, mmawa wotsatira, belu linalira ndipo—ndipo malipenga onse analira, kuyimba kumapitirira, ndipo iye analowa mkati ndipo anamukhazika iye kumbuyo mmbuyo. Iye anabwera kuti adzafufuze chimene icho chinali, choonadi kapena ayi. Iye ankafuna kuti adzafufuze yekha. Iye sanalolere kuti akhale pansu kumeneko. Ngati iye anamva

chinthu chachikulu ichi, iye sakanatenga chimene winawake ananena za icho. Iye ankafuna kuti adzadzifufuzire yekha.

¹⁴¹ Monga Filipino anamuuzza Nataniele, mu phunziro lathu usiku watha, anati, “Kodi chirichonse chabwino chingachokere ku Nazareti?” Kapena kuchokera ku . . . Ine ndiwaganizira malowo mu miniti, kumene Iye anachokerako. Anati, “Kodi chirichonse chabwino chingachokere mu Nazareti?”

¹⁴² Anati, “Bwera udzawone. Usakhale pamenepo ndi kumatsutsa. Bwera, udzadzipezere wekha.”

¹⁴³ Ngati ife titangochita chinthu chomwecho usikuuno. Bwerani, mudzawone! Tengani Baibulo lanu, mufufuze zimene inu mukuziwona zikuchitika. “Fufuzani Lemba,” Yesu anati, “pakuti Iwo ali Iwo amene akuchitira umboni za Ine.” Iye ndi Mawu. Ndipo Malemba Iwoeni ndi Mawu, chotero Iwo amachitira umboni za Iye pamene Lemba likhala Moyo kwa inu, pamene Ilo liwonetseredwa mwa inu.

¹⁴⁴ Tsopano ife tikupeza kuti iye anali atawerenga mipukutu, ndipo iye anadziwa chikhalidwe cha chimene Yehova anali: nzeru zonse. Ndipo pamene iye anamanga mahema ake aang’ono, anaika mphatso zake mmbuyo pa ngodya, kuti akapeze ngati izo zinali zoono kapena ayi. Ngati izo ziri zoono, ndi zoyenera chirichonse chimene iye anabweretsa. Ngati izo si zolongosoka, abwerera nazo izo.

¹⁴⁵ Ndipo ine ndikuganiza chinthu chomwecho usikuuno. Ngati dongosolo ili la chipulumutso limene ife tikulimbanira liri loona, ife tiri ndi ngongole ya chirichonse chimene ife tiri nacho, moyo wathu, nthawi yathu, china chirichonse. Ngati izo si zolongosoka, ndiye kafufuzeni zomwe ziri zolondola; chifukwa iwe umangokhala ndi moyo umodzi uwu, ndipo iwo posachedwapa utha. Fufuzani Malemba, poyamba, ndipo muwone ngati izo zikufanana ndi Lemba.

¹⁴⁶ Ndiye ife tikumupeza mkazi wamng’ono uyu akutenga mpando wake kumbuyo komwe mmbuyo, monga obwera onse atsopano amayesetsa kuti achitire nthawizina. Ndipo lipenga litatha kuwomba. Abusa a Solomoni anadzalowa, nakhala pansi. Msonkhano unayambika. Makadi a pemphero anaitanidwa. Izo zikumveka moipa, koma ine ndikuyesetsa kuti ndipange mfundo. Ndipo iye anapeza tsopano. Iye anati, “Ine ndiwona pamene pali nzeru izi.” Chotero pamene wodwala woyambayo, komabe iye anabwera, kapena chirichonse chimene funso linali, anabwera pamaso pa Solomoni, iye anawulula izo. Iye anati, “Anati, izo nzoona.”

¹⁴⁷ Tsopano, iye sanafune kunena kuti, “Inu mukudziwa, munthu ameneyo ali ndi kuwerenga maganizo, ine ndikukhulupirira.” Mtima wake unayamba kuchita njala. Iye anayamba kukhulupirira, tsiku ndi tsiku.

148 Potsiriza inafika nthawi yake kuti adzaima pamaso pake. Iye anali ndi zinsinsi zina, nayenso. Ndipo pamene iye anabwera pamaso pa Solomoni, Baibulo linanena, kuti, “Panalibe chirichonse mu mtima mwake chimene chinakanizidwa kwa Solomoni.” Iye anawulula chinsinsi chirichonse mu mtima mwake.

149 Ndipo pamene izo zinachitidwa pa iye, iye anaima ngati wachikunja pamaso pa anthu, ndipo iye anati, “Zonse zimene ine ndinazimva ndi zooni, ndi zochuluka.” Iye anati, “Odala ndi amuna omwe amakhala pano kuti aziwona chinthu ichi chikuchitika tsiku lirilonse.” Amen. Oh, iye—iye analibenso mpweya mwa iye, nkome. Pamene iye anawona kuti ena anali nazo izo zitachitidwa pa iwo, ndipo iye anali nazo zitachitidwa pa iye, ndipo anakhulupirira Mulungu.

150 Nzosadabwitsa, nzosadabwitsa kuti Yesu ananena kuti, “Iye adzaima ndi m’badwo uno.” Pamene, apo Iye anali atayima pamenepo, akuchita chinthu chomwecho, kokha zochuluka za izo, ndi zizindikiro zochuluka zamphamvu; ndipo iwo anali ataima pamenepo, “Tiwonetseni,” akuti, “tiwonetseni ife chizindikiro chochokera Kumwamba.” Oh, anthu angakhale akhungu bwanji! Iye anati, “Iye adzaima mu Chiweruzo, ndi m’badwo uno, ndipo adzawutsutsa iwo.”

151 Ndiyeno zitatha zaka thuu sauzande za kulalikira Uthenga, ndi Mzimu Woyera ukutsanulira mmasiku otsiriza ano, pa anthu, mphatso za Mzimu Woyera, ndi kulonjeza kuti kuzindikira kwakukulu uku kudzabwereranso mu mpingo kachiwiri; kodi iye adzachita chiyani kwa m’badwo uno pamene iye adzayime pamenepo, itadutsa nthawi yake kuphatikiza zaka thuu sauzande za kulalikira Uthenga, mmasiku otsiriza ano kuti tiwone zimphatso, osati mphatso, koma zimphatso za Mzimu Woyera? Iye anapereka moyo wake kwa Khristu. Chifukwa chiyani?

152 Ine ndiyenera kuti nditseke, chifukwa ine sindiri...ine ndikufuna—ine ndikufuna kuti ndikupempherereni inu.

Abwenzi, mwaona, iwo anati, “Tiwonetseni ife chizindikiro. Ife tikufuna...”

153 Ndiro limene liri vuto ndi Achipentekoste. Inu mukufunafuna chinachake, ndipo limodzi la masiku awa izo zidzakhala ziri patali kwambiri. Izo zinakudutsani inu pomwepo, ndipo inu simunadziwe izo.

Kumbukirani, mmasiku a Eliya, iwo sanamudziwe iye.

154 Mmasiku a Yohane M’batizi, iwo sanamudziwe iye. Ndipo iye anayankhulidwa, mu Lemba, kuti iye akanadzakhala, “Ine ndidzatumiza mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, kuti adzakonze njira.”

¹⁵⁵ Ndipo ngakhale ophunzira anabwera kwa Iye, anati, “Chifukwa chiyani Eliya ayenera kubwera?”

Iye anati, “Iye anabwera kale, ndipo inu simunazidziwe izo.”

¹⁵⁶ Iwo sanadziwe kuti Yesu anali Khristu, mpaka Iye atafa ndipo ataikidwa mmanda.

Iwo sanadziwe kuti Ireniasi anali kapena . . .

¹⁵⁷ Ine ndinena izi, kuti anthu onse adziwe. Iwo sanadziwe Joan waku Arc anali woyera wa Mulungu, mpaka iwo anamupha iye. Mpingo wa Katolika unamuwotcha Joan waku Arc, ngati mfiti, chifukwa iye ankawona masomphenya ndi kupempherera odwala, ankabweretsa akufa kubwerera ku moyo. Ndipo mpingo wa Katolika unamutcha iye mfiti, ndipo anamuwotcha mkazi ameneyo pa nkhu. Ndipo pafupifupi zaka thuu handiredi mtsogolo, iwo anadzuka ndipo anadzapeza kuti iye anali woyera. Ndithudi, iwo anachita kudzitunduza kwakukulu, iwo anafukula matupi a ansembe aja ndi kuwaponyera iwo mu mtsinje. Zamkhutu!

¹⁵⁸ Koma mupenyetsetse pamenepo, izo zikhoza kuchitika pakati pathu, kuti chinthucho chikhoza kubwera ndi kudzazindikiritsidwa bwinobwino ndi Mulungu mu Lemba, ndi mwa sayansi ndi china chirichonse, ndipo izo zikhoza kudzatidutsa ife ndipo ife osazidziwa izo ayi. Ndiye nkudzaima mu tsiku lotsiriza, kuzindikiritsidwa momveka.

¹⁵⁹ Munthu akadali yemweyo. Munthu nthawizonse amamuyamikira Mulungu pa zomwe Iye wachita, ndipo iwo akuyankhula za zomwe Iye ati adzachite, ndi kumanyalanyaza zomwe Iye akuchita. Ndicho chikhalidwe cha munthu.

¹⁶⁰ Tiyeni tiyang’ane pa Iye, chimene Iye akuchita tsopano. Iye ndi Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Yehova Mulungu yemweyo amene anawonetseredwa mwa Iye. “Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti ine ndinali mwa Atate, ndi Atate mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Mulungu kudzitsitsa kuchokera ku Lawi la Moto, kudzakhala Munthu; ndipo kuchokera ku moyo woperekedwa nsembe wa Munthu ameneyo, Magazi amene anatitsuka ife ndi kudzabwera mwa ife, kuti adzayanjane kachiwiri, kudzawukoka mpingo wa Edeni kachiwiri.

¹⁶¹ Chifukwa chiyani? Tsopano khalani chete miniti yokha. Kodi izi zinachita chiyani kwa mkazi ameneyo? Iye anali wachipembedzo wodzinenera, koma mtima wake unali ndi njala kuti awone chinachake chenicheni. Iye ankafuna chinachake chenicheni.

¹⁶² Ngati inu muli ndi njala kuti muwone chinachake chenicheni, Mulungu adzachisonyeza icho kwa inu. Inu nthawizonse mudzapeza chimene inu mukuchiyembekezera.

¹⁶³ Izo zikundikumbutsa ine, monga anthu nonse inu mukudziwa kuti ine...ine ndinali kuyankhula ndi mzanga kumbuyo kuno, M'bale Brown, kanthawi kapitako. Ine ndikukumbukira Mlongo Brown ali muno penapake, iye anati; mudalitseni iye. Momwe ine ndinkakhalira ndi anthu amenewo kumusi uko mmasiku oyambirira a utumiki wanga! Ndipo M'bale Brown ali ngati m'bale wokwanira-kwathunthu kwa ine, chifukwa iye amakonda kusaka. Mlongo Brown anamugulira iye mfuti yatsopano ya Browning yamakono. Ine ndinamufunsa iye ngati iye anali nayobe iyo. Iye anati, "Inde." Ine ndidzamutembenezira iye kokonda mfuti, limodzi la masiku awa, kumuchotsa ku chinthu chobalalika chakale icho.

¹⁶⁴ Tsopano zindikirani. Koma mu kusaka, ine ndinkakonda kupita ku nkhalango ya kumpoto kukasaka gwape, pamwamba kwambiri, New Hampshire ndi Maine ndipo ndiko kwawo kwa gwape wamchira woyera. Ndipo ine ndinali ndi mzanga kumtunda uko, ine ndinkasaka naye. Ndipo iye anali msaki wabwino, wa pafupifupi kotala ya magazi wa Chimwenye. Ndipo iwe amasowa kuti uzidandaula za iye; iwe sukanamutaya iye, iye amadziwa koti apite. Ndipo iye anali msaki wabwino. Iye timakhoza kulekana, ndi malo amene tingakakomane kutsidya kwa mapiri oyera awo ndi nkhalango zazikulu, koma ife timakhoza kukapezana wina ndi mzake. Ndipo ife sitinali otsalirammbuyo; ife tinkasaka. Ine ndinkakonda kusaka ndi Bert.

¹⁶⁵ Iye anali msaki wabwino, koma iye anali munthu waliuma kwambiri amene ine ndinayamba ndamuwonapo. Munthu ameneyo anali ndi mtima mwa iye ngati mwala. Iye anali wankhanza. Iye anali ndi maso ankawoneka ngati buluzi, ndipo iye—iye—iye anali waliuma basi, mophweka basi waliuma. Ndipo iye anakonda kuwombera agwape, amaneyo ndi mwana wa gwape wamng'ono, basi kungofuna andipangitse ine ndimverere moipa. Iye amakhoza kupha agwape aang'ono awa, ndipo ine ndikudzati, "Bert, kodi iwe sukuchita manyazi kuti ukuchita zimenezo?"

¹⁶⁶ Ndipo iye amakhoza kunena kuti, "Basi ndi momwe alaliki inu mumakhalira, ndinu amtima wankhuku kwambiri."

Ine ndinati, "Bert, umenewo si mtima wa nkhuku. Kumeneko ndi kukhala wankhanza."

¹⁶⁷ Tsopano, ndi zabwino bwino, a—a—mtundu wa agwape kapena kukula kwake. Ngati lamulo likunena kuti iwe ukhoza kupha mwana wa gwape, pitirira ndi kumupha iye. Chabwino, Abrahamu anapha mwana wa ng'ombe ndipo anamudyetsa Mulungu. Panalibe kanthu kolakwika ndi mwanayo wa gwapeyo.

¹⁶⁸ Koma kungowapha iwo ndi kuwasiya iwo pamenepo, basi kungoti ukhale wankhanza, ndiko kupha. Ndipo ine

sindimazikonda zimenezo, ndipo ndimakhoza kumuuzza iye. Ine ndimakhoza kunena kuti, “Bert, iwe ndiwe mzanga, ndipo ine ndimakukonda iwe, ndipo ndiwe msaki wabwino. Ndiwe wowombera wabwino, kuwombera kwabwino, wowombera nkupha.” Ine ndinati, “Ine ndimakukonda iwe, koma—koma ndiwe—ndiwe—wankhanza.”

¹⁶⁹ Ndipo iye ankati, “Oh, Billy, ngati iwe ukanati usakhale mlaliki, iwe ukanakhala msaki wabwino.”

¹⁷⁰ Ndipo ine ndinati, “Tamvetsera, Bert, iwe ukhoza kukhala munthu za izi.” Ine ndinati, “Kumeneko ndi kulakwitsa.”

¹⁷¹ Iye anati, “Iwe. . .” Ine ndinali wolondera zinyama kwa zaka, inu mukudziwa. Ndipo iye anati, “Iwe, iwe unakhalako kosungira zinyama nthawi yaitali.”

Ine ndinati, “Ayi, ine sindinateropo.”

¹⁷² Ndipo chotero tsiku lina ine ndinapita kumeneko kuti ndikasake. Kunali mochedwerapo pang’ono mu nyengoyo. Ine ndinali ndikuchititsa misonkhano ina. Ndipo chisanu chinali chitabwera kale, pafupifupi mainchesi sikisi, chisanu chothandizira kutsatira mphondero. Ndipo ine ndinakumana ndi Bert, ndipo iye anati, “Kuti, Billy, ine ndiri ndi chinachake chatsopano kwa iwe.”

Ndipo ine ndinati, “Chiyani?”

¹⁷³ Iye anasolola mmalaya ake wezulo yaing’ono, ndipo iye anayiriza wezulo yake yaing’ono iyi. Ndipo iyo inkamveka ngati gwape wamng’onoyo akuitana amayi ake, inu mukudziwa, kagwape kakang’ono basi, kulira kwakung’ono uko kumene iwo amapereka.

¹⁷⁴ Ndipo ine ndinati, “Bert, iwe sukutanthauza kundiuza ine kuti iwe ukhoza—iwe ukhoza kuchita zimenezo?”

Iye anati, “Oh, iwe talongosoka, mlaliki.”

¹⁷⁵ Chotero tsiku lotsatira ife tinapita kukasaka. Ndipo ife kawirikawiri timatenga sangweji, ndi—ndi kutenga botolo laling’ono la—la chokoleti chotentha, chifukwa chimakhala ndi shuga mmenemo, inu mukudziwa, ndipo chimatitenthetsa ife. Eya, kumakhala kozizira kwambiri kumeneko, cha mu nthawi imeneyo ya chaka. Chotero ife. . .

¹⁷⁶ Nyengo inali mkati. Ndipo—ndipo pamene iwe uwombera mfuti zingapo, inu mukunena za Houdini kuti anali katswiri pothawa, anali mwana poyerekeza ndi agwape amenewo. Chifukwa, iwo amakhoza kuchokapo pompano, kudzakwawa pansu pa milu ya maudzu kapena chirichonse, ndiyeno nkudzadya usiku ngati mwezi unali kuwala. Ndiye, ngati iwo satero, iwo akanafa ndi njala, iwo asanatuluke, chifukwa iwo ankadziwa kuti inali imfa kuti atulukire kumeneko. Ndipo koteru nyengo inali itatha, anthu anali akusaka kwa masabata angapo.

177 Ndipo ife tinayenda utali wa m'mawa wonse, ndipo ife sitinawone ngakhale njira imodzi. Cha pafupifupi masana, iye anali akuyenda kutsogolo kwanga. Ife tinali tikupita pamwamba pa mphako, ndipo kenako tinalekana ndipo tinadzabwerera njira ziwiri zosiyana, ndipo tinabwera ku msasawo usiku umenewo, mwinamwake kudzalowamo naini, teni koloko. Ngati tipha gwape, ife timamupachika iye, kotero tonse a ife timabwerera tsiku lotsatira ndikukathandiza kuti alowe mkati. Kotero tinali kukukwera mmwamba, kuti tikasiyane, ndipo tinali tisanafikebe pamwamba pa mzere wa mitengo.

178 Ndipo pafupifupi hafu-pasiti leveni kapena thwelovu koloko, Bert anakhala ngati anawerama pansi. Chisanu chinali chikupita mwakuya kwenikweni, pamwamba m'phiri. Ndipo iye anakhala ngati wawerama pansi, ndipo ine ndinaganiza kuti iye anali atafikira mmbuyo. . . Iye sananene zochuluka kwambiri. Ndipo iye anafikira kumbuyo uko, ine ndimaganiza kuti iye amatenga chakudya chake cha masana; ndipo ine ndinapita kukatenga chakudya changa cha masana. Ine ndinaganiza, "Chabwino, ife tidya. Apa ndi pamene ife timasiyana, ndipo iye amapita mozungulira mbali *iyi*, ndipo ine ndimapita mbali inayo."

179 Ndipo iye anakhala pansi. Apo panali polambula papang'ono, pafupifupi kawiri kukula kwa chipinda chino, pang'ono chabe, chimene ife timachitcha, malo ochezerako aang'ono a udzu. Sindinawonepo mphondero mmawa wonsewo. Ndipo iye anakhala pansi pamenepo pambali pa ichi, pansi, pafupi ndi mitengo ina, ngati gombe la chipale chofewa; anafikira mmusi monga *chonchi*, ngati iye akukatenga lake—botolo lake lotenthetsera kapena sangweji yake, anayamba kuitulutsamo iyo. Ndipo ine ndinafikira kwa yanga. Ndipo iye anasolola wezulo yake yaing'ono *iyi*. Ndipo iye anayang'ana mmwamba pa ine, ndi maso a buludzi amenewo.

180 Ndipo analiza wezulo *iyi*. Ndipo pamene iye analiza wezulo *iyi*, iye anakhozadi kuipangitsa iyo kugwira ntchito, iyo inkamveka ngati kamwana kagwape. Ndipo pamene iye anatero, mu kudabwitsidwa kwanga, kudutsa bwalo lolambulidwalo, mayi gwape wamkulu anaimirira. Ameneyo ndi manthu, wamkazi; nyama yokongola, maso aakulu abulauni, ndi makutu amenewo atakwezedwa mmwamba. Ndipo iye anayang'ana mmwamba pa ine, monga *choncho*, ndipo kukhala ngati kumwetulira kopusa. Anayang'ana mmwamba kwa ine monga *choncho*, anadzabwezeretsanso wezulo yakeyo. Ine ndinaganiza, "Bert, iwe sungachite zimenezo."

181 Iye anati, "Shi." Ndipo ine ndinawona. . . Iye anawuziranso iyo kachiwiri, pang'ono kwenikweni, mopepuka.

182 Ndipo, tsopano, zimenezo ndi zosazolowereka kwa gwape ameneyo. Nthawi imeneyo ya tsiku, leveni koloko masana,

kutuluka? Ayi. Chinali chiyani icho? Mwana wake anali mu vuto. Iye anadzuka. Ine ndinamuyang'ana iye, kuseri kwa tchire ili.

¹⁸³ Ndipo iye analiza iyo kachiwiri. Iye anapanga masitepe awiri kapena atatu mtsogolo, akubwera kumene poyera.

¹⁸⁴ Ndizo zonse pamodzi zosazolowereka. Inde, bwana, iye sakanati achite zimenezo. Ayi, bwana. Koma chinali chiyani chimenecho? Mwana wake anali mu vuto.

¹⁸⁵ Ndipo iye anayenda masitepe pang'ono patsogolo, makutu aakulu awo, iye anapotokera cha m'mbali. Ndipo Bert wachikulire anayang'ana mmwamba kwa ine. Ndipo ine ndinaganiza, "Uh-oh." Ine ndinamuwona iye akuyika chipolopolo chimenecho mu mpope wa sarte-ought-sikisi ija, ndi kutsitsira pansu chokhethemuliracho.

¹⁸⁶ Anakweza mmwamba, ndipo mizere yopingasa pa chopenyera cha mfutiyo inadzabwera pa mtima wake. Ndipo pamene anadzaikweza mfuti yake, gwapeyo anamuwona msakiyo. Iye anapotoloka.

Ndipo iye analizanso wezuloyo kachiwiri.

¹⁸⁷ Inu mukudziwa, kawirikawiri gwape ameneyo amakhala atapita. Koma osati iye. Bwanji? Iye anali mayi. Iye sanali kuvala chinachake. Mkati mwa iye, iye anabadwa ali mayi. Mwana wake anali mu vuto. Ngakhale iye ankadziwa kuti izo zikanatengera moyo wake, iye samasamala. Iye anali mayi. Iye sanali kuvala mtundu wina wa zozipangitsa. Izo zinali zenizeni, moyo wake. Iye anali mayi.

¹⁸⁸ Ndipo ine ndinamuwona msakiyo akukoka mfuti yake; ndipo iye anali wowombera wakupha. Ndipo ine ndinatembenuza mutu wanga. Ine sindinakhoza kuyang'ana pa zimenezo. Ine ndinaganiza, "Kodi munthu wankhazayo angaphulitse bwanji mtima wa wantengo wapatali wokhulupirika umene ukugundira khanda lake? Iye angakhoze bwanji kuwuphulitsa mtima wake kuwuchotsa mwa iye?" Ndipo ine ndinadziwa kuti chipolopolo cha machaka okula handiredi-ndi-eyite cha bowa icho chikanasesa mtima wake mpaka kumudutsa iye, pa mtunda umenewo. Ine ndinaganiza, "Iye angakhoze bwanji kuchita zimenezo?" Ndipo ine ndinatembenezira nsana wanga, kuti ndisamayang'ane pa izo.

¹⁸⁹ Ndipo ine ndinayamba kupemphera. Ine ndinati, "Atate Akumwamba, zingatheke bwanji kuti munthu ameneyo akhale wankhaza chomwecho? Mayi wofunika uja, iye sangakhoze kudziletsa izo. Iye sikuti akuchita kuvala ngati chiwonetsero. Iye ndi weniweni. Ndipo iye ali—ndipo iye ndi mayi, ndipo iye akuitanidwa, akuyesetsa kuti amupeze mwana wakeyo. Ngakhale izo zitengere moyo wake, mwana wake ali mu vuto." Ndipo ine ndinali ndikupemphera, kwa inemwini, kumamvetsera nthawi iliyonse kuti ndimva kukhethemula kwa moto, ukugwa, ndipo mfuti imeneyo ikuwomba. Ndipo ine

ndinali nditangoima pamenepo nditadzigwira ndekha monga *chonchi*, ndikupemphera.

¹⁹⁰ Ine ndinadikirira, ndinadikirira. Mfutiyo siyinaphulike. Ine ndinadikirira mphindi chabe. Ndipo ine ndinatembenuka kuti ndiyang'ane, ndipo iye anali akupita monga *chonchi*. Iye amalephera kuti ayigwire mfutiyo mosasuntha. Ine ndinayang'ana pozungulira pa iye.

¹⁹¹ Iye anayang'ana mmwamba kwa ine. Nkhope yake inali itasintha. Maso abuluzi awo anali atagwera ku chinachakenso. Misonzi inali ikutsikira mmasaya ake. Iye anaponyera mfutiyo pansi. Iye anati, “Billy, ine ndakhala nazo zokwanira za izi. Ndisogolere ine kwa Yesu uyo yemwe iwe ukumukamba.”

¹⁹² Kumeneko pa mulu wa chipale, madzulo amenewo, ine ndinamutsogolera munthu wantima wankhanza uja kwa Yesu Khristu. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anawona chinachake chenicheni, chinachake chimene sichinali chovala, chinachake chimene chinali chenicheni.

¹⁹³ Oh, dziko la njala ili likufunafuna chinachake chenicheni, chinachake chimene sanachite kuvala, chinachake chimene chiri chenicheni, chimene chiri chobadwa mwa Mulungu, chimene chimachokera mu Baibulo. Kodi inu simungatero, madzulo ano, amayi, m'bale; kodi inu simungatero, Mkhristu, monga kukhala naye Yesu Khristu mu mtima mwanu, Mzimu wa Mulungu wochuluka mu mtima mwanu, umene ungakutsogolereni inu kuti muzichita zinthu zokhulupirika monga momwe gwape uja anachitira ndi mwana wake? Kodi inu simungakonde kukhala Mkhristu wa mtundu umenewo? Kodi inu mungafune kuti mukhale ndi chipulumutso cha mtundu umenewo chimene chingati . . . inu . . . imfa kapena china chirichonse, ndipo basi—chikondi cha Mulungu mu mtima mwanu, monga iye anali ndi chikondi cha mwana wake?

¹⁹⁴ Tsopano njira yokha yomwe izo zingakhoze kukhalira. Inu simungakhoze kuchita izo pojowina tchalitchi. Inu simungakhoze kuchita izo poika dzina lanu pa bukhu. Izo ziyenera kukhala zenizeni. Izo ziyenera kukhala zenizeni. Uko kuyenera kukhala kubadwa. Izo ziyenera kukusinthani inu, kuchoka ku kungodzipangitsa kukhulupirira, kudzakhala Mkhristu weniweni.

¹⁹⁵ Inu munati, “Kodi inu mukuganiza kuti chikondi chikhoza kukhala chachikulu chomwecho? Kodi inu mukuganiza kuti Iye akhoza kundikonda ine?”

¹⁹⁶ Iye anati, “Mayi akhoza kuiwala mwana wake woyamwa, koma Ine sindingathe kukuiwalani inu. Maina anu anazokotedwa pa zikhatho za dzanja Langa.”

¹⁹⁷ Mulungu anabwera ku dziko lapansi, mmawonekedwe a Munthu, ndipo—ndipo—ndipo anadzadzifutukula Yekha, anadzafunyulula hema Wake; kuchoka pakukhala Yehova

Mulungu, kudzakhala Munthu, kuti adzapirire nawo manyazi ndi themberero. Yehova Mulungu wamng'ono mu khola, pansi pa mulu wa manyowa, kumusi uko akulira modyera ng'ombe; Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, atayima pamenepo mu mnofu wa munthu, kuti adzatenge imfa ya machimo anu pa Iyemwini, kuti Iye adzakhoze kukumasulani inu kuti mukhale Mkhristu mochulukana kuposa chimene gwape ameneyo anali mayi. Inu mungakane bwanji chikondi chosafanizitsidwa choterocho? Ndiye, pambali pa zimenezo, Iye analemba Mawu Ake. Zimenezo ndi zokwanira. Inu mukhoza kulephera kutenga mawu anga, inu muyenera kutero. . . izo zingakhale zabwino, koma osati Iye. Iye anakwera Mmwamba ndipo anapereka mphatso kuzibweza kwa anthu. Iye anabwereranso mmawonekedwe a Mzimu Woyera, Mulungu yemweyo, kuti adzatsegule mtima wanu, mwa Magazi otetezera.

¹⁹⁸ “Khalani inu chotero angwirowo, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali angwirowo.” Palibe mmodzi wa ife angakhoze kukhala chimenecho. Ine sindimayang'ana pa chimene ine ndiri. Ine, ine sindiri woyenera. Inu simuli woyenera. Ndani ali woyenera? Ine sindimayang'ana pa chimene ine ndiri; ine ndimayang'ana ku chimene Iye ali. Iye ndi Mmodzi amene amayang'anidwa. Iye ndi Nsembe yanga. Ine sindiri woyenera kuyima pano ngati mtumiki. Ngati ine ndikanawerengera kuyenera wanga, ine—ine ndikanakhala ndiri ku Gehena, chomwechonso inu. Koma ife sitimayang'ana ku chimene ife tiri.

¹⁹⁹ Inu mukuti, “Ine sindingakhoze kuchita zimenezo. Ine sindingakhoze kuitana. Ine sindingakhoze kukhudza chovala cha Mulungu. Ine sindingakhoze kuchita *izi*.”

²⁰⁰ Oh, inu mukhoza! Taonani zimene zinachitika? Iye anafa, pofuna kuti inu mudzakhoze kuchita zimenezo, kuti inu mudzakhoze kupulumutsidwa. Izo ndi zenizeni. Kodi inu mungafune kuti mukhale monga chomwecho, ndipo mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero? Kwezani dzanja lanu, nenani, “Ine ndingatero, M'bale Branham.”

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

²⁰¹ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, bwerani mokoma, modzichepetsa tsopano. Ife tiribe malo pano oyitanira ku guwa. Palibe ngakhale guwa. Koma Baibulo linati, “Onse amene anakhulupirira, anabatizidwa.” Kuitanira kuguwa, kunabwera mu tsiku la Methodisti, zimene ziri zabwino. Koma mu nthawi ya Ambuye wathu ndi atumwi, iwo “ankakhulupirira ku Moyo.” Iwe unali “kupulumutsidwa mwa chikhulupiriro, kupyolera mu chisomo.” Ngati inu mulibe chokuchitikirani chimenecho usikuuno, m'bale, mlongo!

²⁰² Akazi, ngati inu mulibe chisomo chokwanira mu mtima mwanu, usikuuno, kudziwa kuti Baibulo limaphunzitsa kuti inu musiye kumeta tsitsi lanu, kumavala zazifupi ndi

zodziphoda! Ngati inu mulibe chisomo chochuluka chomwecho mu mtima mwanu, usikuuno! Ndipo inu mukudziwa kuti Baibulo limaphunzitsa kuti inu mukuyenera. Iye sangakhoze kusintha. Inu mukuti, “Ine sindimavala zazifupi. Ine ndimavala mathalauza.” Ndizo nyanyi.

²⁰³ Mulungu anati, “Mkazi yemwe adzavale chovala choyenera mwamuna, ndi chonyansa kwa Mulungu.”

²⁰⁴ Ndipo inu amuna amene simungasiye kupotoloka ndi kuyang’ana pa akazi ovala mopanda khalidwe, mafano a tsiku lino! Iwe mwamuna yemwe ulibe chisomo chokwanira chenicheni mu mtima mwako kuti uwapange akazi ako ndi ana asiye kusiya kuchita chinthu chotero monga icho, chikondi cha Mulungu sichinazikike mu mtima mwako; usati udzitchedwa mwana wa Mulungu. Iwe ukadali mu Sodomu, mwamuna yemwe sangathe kutenga nyumba yake yomwe; Mulungu anamudzozzeratu iye kuti adzatero.

²⁰⁵ Ndipo inu madikoni amene mwakwatira kawiri kapena katatu! Ndipo mwamuna iwe amene mumawazembera azikazi anu, ndi kumayesetsa kugwira chodzinenera chanu! Akazi inu amene munawolokera mbali inayo! Anthu inu amene mumabisala kuseri kwa chovala cha mpingo! Chipembedzo chanu sichidzakhala ndi chochita ndi munthu winayo, musiyeni iye akhale Mkhristu kapena ayi; ngati iye siali wa gulu lanu, inu simudzakhala ndi chochita naye iye. Manyazi pa inu!

²⁰⁶ Mulungu atadziwonetsera kwenikweni, usikuuno, kwa inu. Mulole inu mubwere kwa Iye, mokoma tsopano, ndi kuti, “Ambuye, mundikhululukire ine chifukwa cha machimo anga. Kuyambira usiku uno, mpakana, ine ndidzakutumikirani Inu.”

²⁰⁷ Inu amene mumakonda purogramu ya televizioni, mpaka kuti inu mumatsala kunyumba kuti muwonere katswiri wina wopanda khalidwe wa pakanema monga *Ife Timakonda Susie* kapena zina za zinthu zina izo zimene iwo ali nazo, kutsala kunyumba Lachitatu usiku kuti muziwonera televizioni mmalo mobwera ku chipinda chopempherera, chikondi cha Mulungu chachoka mu mtima mwanu. Inu mumachita zimenezo, ndipo komabe inu mumagwiritsitsa umembala wanu? Chikondi cha Mulungu chingakuchotseni inu kuchoka kwa zimenezo, ndi kukuthamangitsirani inu ku mpingo wanu, kwa wanu—m’bale wanu ndi mlongo; kubwera pamodzi, kudzakhala mmalo Ammwambamwamba ndi kudzamvetsera kwa abusa anu akulalikira. Ndipo chi—chitsitsimutso, kapena msasa, ukutha tsopano. Ngati izo zikukhalabe mu mtima mwanu, tiyeni tipemphere limodzi tsopano kuti Mulungu azichotse izo.

²⁰⁸ Ambuye Yesu, ife tikubwera ndi kukhudzidwa modzichepetsa, ife tikubwera ndi mitima yolapa, Ambuye. Ife tonse ndife olakwa. Ife talakwira Malamulo Anu. Ife talakwira malamulo a chikondi Chanu chimene chinatipulumutsa ife.

Mpingo pawokha wayamba zonyanyuka ndi madongosolo azomanga, ndi mitundu yonse ya zinthu; ndipo unasiya msonkhano wa pemphero ndi—ndi Mzimu Woyera unayamba chinachake cha kamodzi kapena kawiri pa sabata, pamene izo ziyenera kukhala mmitima yathu ndi malingaliro mowirikiza. Tikhululukireni ife, Ambuye.

²⁰⁹ Muwakhululukire azitumiki athu, Ambuye, amene amaima pa guwa ndi kuchita manyazi kuti anene Uthenga wathunthu wa Khristu. Ndi momwe kuti ambiri a iwo lero. . . Dziko lonse lasanduka Sodomu. Atumiki ambiri akhala mu parishi yawo, usikuuno ndi mawa, kapena kowerengera kwawo, kuyesetsa kuti apeze mawu; ndi kuyendetsa Mawu a Mulungu, ndi kumawona machimo, koma amawopa kuti anene chirichonse chokhudza izo, chifukwa iwo angachotsedwepo. Gulu la madikoni lidzawaitanitsa iwo, ndipo lidzawapititsa ku malikulu ndi kukachotsedwako, pamene iwo akudziwa kuti iwo ayenera kulalikirira motsutsa tchimo. Ndi Loti, kachiwiri, “Machimo a Sodomu anasautsa moyo wake wolungama.” Koma munthu alibe kulimbamtima. Chimodzimodzi monga Loti, iye analibe kulimbamtima kuti aimirire.

²¹⁰ Ine ndikupemphera, Mulungu, Inu mutikhululukire ife chifukwa cha zinthu zoterozo monga zimenezo. Mulole ife tikhale monga Paulo wakale, “Ine sindinaleke kukuuzani inu uphungu wonse wa Mulungu.” Tikhululukireni ife tonse, Atate.

²¹¹ Monga nkhani yophweka yaing’ono iyi, ya tsiku lozizira la Novembara lija, pamwamba pa phiri ilo pamenepo; momwe munthu ameneyo, usikuuno, dikoni mu mpingo kumeneko, Mkhristu wokhulupirika, chifukwa mayi gwape anatulukira ndipo anawonetsa chinachake chenicheni. Inu munati, “Ngati—ngati iwo akhale bata, miyala idzafuula mokweza.”

²¹² Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mutipatse ife chinachake chenicheni kwambiri, usikuuno, chimene chiti chikopere tcheru chathu kwa Khristu, kutidziwitsa ife kuti Iye ali pakati pathu, usikuuno.

²¹³ Manja olapa anakwera mmwamba, mahandiredi a iwo. Akhululukireni iwo, Ambuye. Tsopano ine ndikukukumbutsani Inu, Ambuye, za Lemba limene Inu munati, “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Iwo angakhoze bwanji kukweza manja awo kupatula Inu mutawakoka iwo? Pamene iwo akukweza manja awo, iwo amaswa lamulo la sayansi lililonse. Mphamvu yokokera pansi imagwirira manja awo pansi. Koma munali mzimu mwa iwo, ndi cha Mzimu pa iwo, chimene chinati, “Iwe ukulakwitsa. Kweza mmwamba manja ako.” Ndipo icho chinanyoza malamulo a mphamvu yokokera pansi, ndipo anakwezera manja awo kwa Mlengi, “Ndichitireni ine chifundo, Mulungu.”

²¹⁴ Ndipo Inu munati, “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine. Ine mwanjira iliyonse sindidzawaponyera iwo kunja. Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya, ndipo ndidzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza.” Inu munati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera konse ku Chiweruzo, koma wadutsa kale kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.”

²¹⁵ [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]...ku Ufumu wa Mulungu, kuti apange mamembala omvera a Thupi la Khristu. Ndipo mipingo yawo, ya atumiki awa, ikhoza kukula ndi kukula ndi mamembala, obadwa mwatsopano, mu Ufumu wa Mulungu. Adalitseni abale anga, kuti aliyense amene iwo akumupempherera achiritsidwe; Uthenga umene iwo akulalikira, osati ukagwere polimba, nthaka ya miyala, koma pa mitima yofewa.

²¹⁶ Perekani izi, Ambuye, kuti Ufumu wa Mulungu posachedwapa ukhazikitsidwe mdziko lapansi. Inu mukudzera nthumwi Zanu. Tsiku lina Mwanawankhosa adzachoka ku malo opatulika, adzabwera kudzatenga Bukhu kuchokera mdzanja la Iye Amene ali Mwini wa chikalata cha izo. Pamene munthu analakwa, ndipo Bukhu la Moyo linabwerera kwa Mwini wake wapachiyambi. Munthu, moyo wonse unatayika; ndipo panalibe munthu, Kumwamba kapena pa dziko lapansi, amene anali woyenera. Koma a—Mwanawankhosa anatulukira, Mwanawankhosa Wamagazi amene anali ataphedwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, amene anabwera ndipo anadzatenga Bukhu la Chiwombolo ndipo analitsegula Ilo. Mulungu, mulole dzina langa likhale pamenepo. Mulole dzina lililonse pano lilembedwe Pamenepo, Ambuye, lomwe linawomboledwa mu dongosolo lalikulu ili la chiwombolo. Perekani izi, Atate.

²¹⁷ Ndipo tsopano ife tikuwapereka iwo kwa Inu. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Ndipo ngati alipo aliyense pano amene sanabatizidwepo mu ubatizo wa Chikhristu, mulole iwo abwere patsogolo, mwa kuchita kwa chikhulupiriro, ndipo adzavomereze kuti iwo akulakwitsa, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo awo, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Perekani izi, Atate.

²¹⁸ Kodi Inu mutimva ife, Atate, pa pemphero ili, pamene ife modzichepetsa tikulipereka ilo kwa Inu, mu Dzina, Dzina lokwanira mu zonse limene Miyamba yonse ndi dziko lapansi zimatchedwa, Yesu Khristu. Amen.

Pali Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
Ochokera mmitsempha ya Emanuele,
Ndipo ochimwa amadziponyera pansu pa
kusefukirako,

Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse.

Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse,

Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse;

Ndipo ochimwa amadziponyera pansu pa
kusefukirako,

Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse.

219 Kodi inu simumazikonda nyimbo zakale zimenezo? Zipitiriranibe. Kodi izo si zodabwitsa? Zolembedwa ndi Mzimu Woyera. Ine ndimangozikonda izo. Ine ndikuganiza nyimbo za chisangalalo ndi zabwino, koma ine ndimakonda nyimbo zakale izi za Magazi, nyimbo za Chikhulupiriro. Tiyeni tiyimbe iyo, ndime ina, kayimbidwe-kachikale, mwa kumudzi, momwe ife tinkaimbira iyo mmbuyo ku mapiri zaka zapitazo.

Wakuba pakufa anasangalala kuwona (mwayi
Wake wotsiriza.)

Kasupe ameneyo mu tsiku lake;

Pamenepo mulole ine, ngakhale woyipa monga
iye,

Anatsuka machimo anga onse.

220 Tiyeni titseke maso athu ndipo mokoma tiyimbire iyo kwa Khristu.

Wakuba pakufa anasangalala kuwona

Kasupe ameneyo mu tsiku lake;

Ndipo apo mulole ine, ngakhale woyipa monga
iye,

Mutsuke machimo anga onse.

Mutsuke machimo anga onse,

Mutsuke machimo anga onse;

Ndipo apo mulole ine, ngakhale woyipa monga
iye,

Mutsuke machimo anga onse.

221 Oh, kodi izo sizikukupangitsani inu kumverera kuti mwakwechedwa mkatimo, mukungomverera kukoma kwa Kukhalapo kwa Mulungu? “Tsopano inu ndinu ana a Mulungu. Tsopano ife takwezedwa mmwamba mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu,” ndi ulamuliro wonse, Miyamba ndi dziko lapansi zaperekedwa kwa ife. Kodi inu munayamba mwaganizapo za zimenezo?

Winawake akuti, “Kodi inu muli nayo mphamvu iliyonse?”

“Ayi, koma ine ndiri nawo ulamuliro.”

222 Ziri monga wapolisi wamng’ono ataima kunja kuno pa msewu, kamunthu kakang’ono kamene kali ndi chipewa chokokedwera mmakutu ake, wolemera pafupifupi mapaundi handiredi, baji itamatidwa pa iye. Ndipo apa pakubwera mulu wa magalimoto pa msewu, akuyenda mamailosi handiredi pa ora; imodzi iliyonse ya iwo, mphamvu za akavalo foro kapena

faivi handiredi. Iye sangakhoze kuyimitsa imodzi ya izo. Koma muloleni iye aimike mmwamba dzanja limenelo. Uh-huh. Iye ali nawo ulamuliro. Ndicho chimene chimapangitsa buleki kulira. Si mphamvu yake. Ndi ulamuliro wake.

²²³ Ndipo ife tiri nawo ulamuliro, mwa Yesu Khristu. Ndi chifukwa chake ziwanda zimafuula. Mukuona? Osati chifukwa chakuti ife tiri nayo mphamvu, koma ife tiri nawo ulamuliro. Mzimu Woyera uli pano, ulamuliro wa Mulungu. “Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inunso mudzazichita.” “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ine ndimamukhulupirira Iye.

²²⁴ Tsopano ife tikukhala mmalo Ammwambamwamba, mu Kukhalapo kwa Khristu, titanyamulidwira mmwamba pamwamba pa zosamalira za mdziko, kukalowa mu dera la chikhulupiriro. Chingachitike ndi chiyani pano usikuuno? Pakhoza kukhala Pentekoste ina. Pakhoza kukhala chinthu choterocho chikuchitika pomwe pano, usikuuno, monga izo zinachitikira mu Machitidwe 2. Ndiko kulondola.

²²⁵ Khristu ali pano. Ngati ife tingakhoze kukuchotsa kuwuma kwa mitima yathu! Kodi Iye ali ndi ife? Kodi izo nzoona? Kodi Khristu ali pakati pathu? Iye analonjeza kuti adzatero. Inu mudzamudziwa chotani Iye? Osati momwe Iye ankawonekera, koma mwa ntchito zimene Iye ankachita. Ndicho chimene Iye analonjeza, ndipo Iye anati Iye akanadzachita izo.

²²⁶ Mulungu, tithandizeni ife usikuuno, kuti pamene ife tizichoka pano, pemphero langa ndiro. . . Ndipo ine ndingonena ilo ndi maso anga otseguka, kwa inu anthu. Ine ndikupemphera kuti inu muwone chinachake chenicheni kwambiri, kuti Mulungu achita chinachake chenicheni kwambiri, usikuuno, mpaka inu mudzanena monga iwo amene ankachokera ku Emmau, pamene inu muzipita ku nyumba zanu, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu?” Mwaona, iwo anali. . .

²²⁷ Yesu anali atapachikidwa, ndipo anafa, anaikidwa mmanda, mpheketsera inali yakuti Iye anali ataukanso kachiwiri, ndipo Iye anayenda nawo iwo tsiku lonse ndipo iwo sanamudziwe Iye. Iye wayenda ndi anthu ambiri, iwo sanadziwe zimenezo. Ndi Yemwe anamuletsa *iye* kuti asakhale ndi ngozi ija akubwera cha kuno; ndicho chimene chimamuchiritsa mwana *wanu*; Khristu, ndipo mwinamwake inu simunachizindikire icho.

²²⁸ Koma usiku wina Iye anawapeza iwo ku Emmau, Kleopa ndi mzake, ndipo iwo anatseka zitseko, ndiye Iye anachita chinachake basi momwe Iye ankachitira izo kupachikidwa Kwake kusanachitike. Iwo anadziwa kuti anali Iye, mu chiukitsiro Chake. Mwamsanga iwo anapita kukawauza ena.

²²⁹ Mulole Iye achite chinachake usikuuno, monga Iye anachitira kupachikidwa Kwake kusanachitike, kwa ife; kuti ife, pamene ife tizipita kuchokera ku Emmau, kuti ife

tikakhoze kuwauza enawo, “Mitima yathu inatentha mkati mwathu.” Mulole ife tiwone chinachake chenicheni, osati mochuluka kwambiri za chiphunzitso china chatsopano kapena chinachake; koma chiphunzitso, chimene ife tikuchidziwa, chikuwonetseredwa mwa mphamvu ya Mulungu.

²³⁰ Usiku wathawu ine ndinaitana mzere wa pemphero, apo panabwera, dona wolumala ndi ena otero, achiritsidwa. Maumboni! Zazin’ongo basi; ife tiyenera kukhala pano pang’ono pokha, osati mokwanira nkomwe kuti tikudziweni inu. Mmenemo ine ndimakhoza kugwira kumverera kwa anthu, akuti, “Iye akuwerenga maganizo awo.” Ine ndinayesetsa kutembenezira nsana wanga kwa anthu ndi kukuwonetsani inu kuti sikunali kuwerenga maganizo.

²³¹ Ambiri a inu a nthawi-zakale kuno mu Arkansas mukukumbukira pamene ine ndinkagwira dzanja la munthu, momwe Iye anandiuzira ine, “Izo zidzafika pochitika pamenepo, kuti ngati uti udzakhale woonamtima, iwe uzidzadziwa chinsinsi kumene cha mtima wawo.” Inu mukukumbukira zimenezo, nonse a inu? Ndipo zinthu zimene Iye wachita, kuzungulira dziko lapansi, kulikonseko!

²³² Musaiwale za *Life* magazine tsopano, mwezi wathawu. Kuwona pamene Iye ananeneratu zomwe zikanati zidzachitike, ndipo apo zayima pamenepo, mboni pano usikuuno zomwe zinali kumeneko. Ngakhale sayansi siikudziwa kanthu za zimenezo. Iwo akudabwa chifukwa chimene izo zingakhalire; koma ndi zimenezo.

²³³ Tsopano, taonani, ine nditenga Lemba latsopano usikuuno. Baibulo linanena, kuti, “Yesu Khristu ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu.” Ndi kulondola uko, abale? Ndiro Lemba. Tsopano, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu, tsopano ngati inu mwamukhudza Iye, Iye akanati achite, ngati Iye ali yemweyo monga Iye analiri, Iye akanati achite monga Iye anachitira nthawi imeneyo. Chifukwa inu simungathe. . . Ndiyo njira yokhayo imene inu mungamudziwire Iye, ndi momwe Iye akuchitira. Mukuona?

²³⁴ Wachinyengo aliyense akhoza kuika zipsyera mdzanja lake, ndipo magari kapena chinanso, koma moyo ndi umene umawauza iwo. Mukuona? Ine ndikhoza kutenga mtengo ndi kumangirizira masamba pa iwo, kunja kuno, a mtengo wosiyana, koma kodi iwo ubala chipatso cha mtundu wanji? Mukuona?

²³⁵ Tsopano, Moyo wa Khristu umakhala mwa iwe, ndiye ngati Moyo woyamba uja umene unachokera mu nthambi imeneyo. . . Tsopano Iye alibe manja tsopano koma anu ndi anga. Iye alibe liwu koma langa ndi lanu. Mwaona, mpesa sumabala chipatso. Nthambi imabala chipatso. Ndipo ngati nthambi imene inabereka pa nthambi yoyamba imene inatuluka kuchokera mu

mpesa wa manyumwa umenewo, monga ine ndinanena, iwo analemba Bukhu la Machitidwe kumbuyo kwake. Ngati iwo uti udzatulutse konse mpesa wina wapachiyambi, inu mudzalemba Bukhu lina la Machitidwe kumbuyo kwake. Iwo udzakhala Mzimu womwewo, chifukwa iwo ndi Moyo womwewo mu mpesa wonsewo. Nthambi iliyonse yomwe idzabala idzakhala Kumeneko.

²³⁶ Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinachake, pamene ife takhala pano. Ndi angati a inu mukukhulupirira kuti Khristu ali pano? Ndi angati a inu akudwala? Kwezani manja anu. Ndi angati a inu mukukhulupirira kuti inu muli ndi chikhulupiriro chokwanira, kuti inu mukhoza kukhudza chovala Chake, Iye akachita mwanjira yomweyo?

²³⁷ Ine sindiyitana mzere wa pemphero. Ndizingoyitanira izo, kungozisiya zizibwera kuchokera kuno. Ndiko kudzibetchera ndithu. Koma inu muli ndi chikhulupiriro chochuluka, ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mulungu achilemekeza icho.

²³⁸ Tsopano ine ndiyang'ana pa omvetsera, ndipo ine ndikufuna kuti ndiwone ngati alipo winawake amene ine ndikumudziwa mwa omvetsera. Ine ndikumudziwa M'bale Tracy Boutliere wakhala apo. M'bale uyu apa, ine sindikuwadziwa atumiki awa omwe ali pomwe apa. Mtumiki mmodzi kumbuyo uko yemwe ine ndikumudziwa iye. Kunja kwa zimenezo, pa ulamuliro wa Baibulo langa, ndipo Ilo pa mtima wanga... Ine sindimalumbira, chifukwa Baibulo linati ndisamachite zimenezo; koma ndi Baibulo langa pa mtima wanga, ine sindimana ayi. Ine sindikumuwona munthu mmodzi winanso amene ine ndikumudziwa, kupatula Jim Maguire.

²³⁹ Ndipo ngati ine sindikutsimikiza, uyo ndi m'bale yemwe ine ndinakomana naye ku kachisi tsiku lina. Ine ndinangokumana naye iye. Ine ndaiwala kuti dzina lake ndi ndani. Iye ndi... amagwira ntchito ku kachisi ku Jeffersonville. Ndi kulondola uko? Tsopano, ameneyo ndi munthu yekhayo amene ine ndikumudziwa, amene ine ndikukhoza kumuwona kuti ine ndikumudziwa.

²⁴⁰ Tsopano, ngati Yesu akanakhala pano, ndipo inu mumafuna kuti muchiritsidwe, ndipo inu mukanati mumufunse Iye, "Ambuye, kodi Inu mungandichize ine?"

²⁴¹ Apa pali chimene. Ngati Iye akanati waima pano atavala suti iyi imene Iye anandipatsa ine, Iye sakanakhoza kukuchizani inu. Iye anachita kale izo. Mwaona, izo zinatsirizidwa pa Gologota. Ndipo dziko lonse linapulumsidwa, dziko lonse linakhulukidwa, chirichonse chinachitika pa Gologota. Mwaona, "Iye *anavulazidwa* chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife *tinachiritsidwa*," tensi yakale. Mukuona?

242 Tsopano chinthu chokhacho chimene inu muyenera kuchita. Izo sizidzakuchitirani inu ubwino uliwonse kupatula ngati inu mutakhulupirira izo; osati kuzimverera izo. Yesu sananene konse kuti, “Kodi munazimverera izo?” Iye anati, “Kodi inu munakhulupirira izo?”

243 Ine ndawawonapo anthu akukweza mmwamba dzanja lawo, ndikuti, “Tazimvererani izo! Tazimvererani izo! Tazimvererani izo!” Iye sananene konse zimenezo.

Iye anati, “Kodi inu munakhulupirira izo?” Chikhulupiriro, mwaona.

244 Zindikirani, tsopano. Ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo, Iye akuyenera kuti adzachite mwanjira yomweyo. Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe Iye akanati andidzoze ine, Iye ayenera kuti akudzozeni inu, aponso.

245 Mukuti, ine ndikuwona munthu amene ine ndikumudziwa. Apo pali Bambo Way, munthu amene anagwa nkufa mu tchalitchi tsiku lina, amene Mulungu anamubwezera ku moyo, wakhala apo pomwe. Ndipo mtumiki wakhala pafupi ndi iye, yemwe ine ndikumudziwa, wakhala apo pomwe pafupi ndi iye. Koma apo ayi, izi. . .Inde, ine ndikukhulupirira ine ndikumuwona m’bale uyu, uyu ndi m’bale wake yemwe ine ndinakomana naye kumusi uko ndi banja la a Blackwell lero, akupemphera mnyumba.

246 Koma anthu inu amene mukumukhulupirira Iye, ndipo mukukhulupirira kuti inu mukhoza kumukhudza Iye, ine ndikufunsani inu chinachake. Tsopano, ndine m’bale wanu, basi a—a—munthu, chimodzimodzi monga mwamuna wanu, kapena m’bale wanu, kapena m’busa wanu, munthu chabe. Ndipo tsopano, pamenepo, izo siziri uko mchipinda china cha mdima, monga mdierekezi wina. Ndipo, mdierekezi samachita zimenezo, mulimonse. Kodi inu munayamba mwamumvapo mdierekezi akulalikira Uthenga, kupulumutsa miyoyo ndi kuchiritsidwa? “Ngati Satana angakhoze kutulutsa Satana, ndiye ufumu wake wagawanika modzitsutsa iyemwini,” Yesu anatero. Ayi.

247 Koma pomwe apa, inu muyang’ane ndi kukhulupirira kuti Yesu akadali Wansembe Wamkulu yemweyo amene Iye anali, ndipo munene kuti, “Ambuye Yesu, ine ndikudwala. Kapena, ine ndiri ndi amayi odwala akhala apa, kapena m’bale kunyumba. Ambuye, ine—ine—ine ndikulephera kulipira ngongole yanga. Ndithandizeni ine. Ine ndi—ine ndikuvomereza machimo anga onse. Ine—ine—ndine wochimwa; ine—ine ndikufuna kuti ndiyanjane ndi Mulungu.” Chinachake chimzake, mufunseni Iye. Mumukhudze Iye, monga Wansembe Wamkulu, ndipo muwone ngati Iye sachita lero monga Iye anachitira nthawi imeneyo. Izo zikusonyeza kuti Iye ali ndi ife.

248 Tsopano, ine ndikukhulupirira Iye achita zimenezo. Ine sindima. . . Iye sanayambe wandilepherapo ine panobe, mu zaka

zonse izi. Ine—ine ndikumukhulupirira Iye. Koma inu mukhoza kumvetsa chimene kudzibetchera kumeneko kuli. Koma izo si . . .

Winawake anati, “Kodi inu simumachita mantha?” Ayi, bwana.

²⁴⁹ Ine ndingachite bwanji mantha, ndipo Iye ali pomwe pano pafupi ndi ine? Iye, ndi Mawu Ake; si anga. Ine ndikungonena zimene Iye ananena, uko ndi kuvomereza kwanga. *Kuvomereza* kumatanthauza “kunena chinthu chomwecho.” Lemba, limene liri Mulungu, Mulungu mmawonekedwe a chilembo. “Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo Mawu akadali Mulungu. Ndipo Mawu anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ziri kwa Iye kuti awatsimikizire Iwo. Iwo ndi woyenera ine kuti ndiwakhulupirire Iwo. Tsopano muwakhulupirire Iwo.

²⁵⁰ Tsopano ine ndikufuna aliyense wa inu ndiye, mwakachetechete, mwabata, kuti mupereke pemphero kwa Mulungu, ndikuti, “Ambuye Mulungu, ndithandizeni ine. Ine ndikudziwa bambo wamng’ono wokalamba wa mapewa akugwa waima pamwamba apo sakudziwa kanthu za ine, koma Inu mukundidziwa ine. Ndipo ngati Inu mutangoti muchite, ndi kubwereza Lemba kwa ine usikuuno.”

²⁵¹ Monga mkazi anakhudza chovala Chake. Iye sanamverere kwenikweni kukhudza kwa dzanja, chifukwa, monga ine ndinakuuzirani inu, chovala cha chi Palestina ndi chomasuka; chovala chamkati, chokhuthala. Miinjiro yaikulu yolembera, Iye sanamverere izo. Ndipo Iye anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

²⁵² Ndipo Petro anamudzudzula Iye, akuti, “Ambuye!” Bwanji, iye anamutenga Iye ndipo anakamudzudzula Iye chifukwa cha zimenezo. Mwakuyankhula kwina, “Izo zikumveka zamisala kuti Inu munene zimenezo. Aliyense akukugwirani Inu ndi mikono yawo, akukusisitani Inu pa nsana. ‘Ndani wandikhudza Ine?’”

²⁵³ Iye anati, “Koma ukoma wachoka mwa Ine. Winawake wandikhudza Ine ndi kukhudza kosi yana.”

Kodi inu mungapange kukhudza kumeneko usikuuno?

²⁵⁴ Ine ndikudzipereka ndekha. Tsopano kumbukirani, ndine wosayankhula kwathunthu kwa zinthu izi, kunja kwa Ufumu wa Mulungu. Ziri monga ngati choyankhulira ichi. Choyankhulira ichi sichingakhoze kuyankhula; icho chikhoza kungoyankhula pamene chinachake chikuyankhula kudzera mwa icho. Ndipo ife tangokhala ngati choyankhulira chimenecho, kwa izi. Ine sindikukudziwani inu, koma zitengera chinachake kuti chiyanhuliremo pano.

²⁵⁵ Ndipo inu mukukhulupirira zimenezo, ndipo mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo Mulungu apereka izo. Kodi

inu mukukhulupirira zimenezo? Tsopano mungokhulupirira. Mukhale ndi chikhulupiriro, ndipo musakaikire. Mukhulupirire pa Ambuye Mulungu. Tsopano mungopemphera, mukhale molemekeza kwenikweni, ndipo mungowona.

²⁵⁶ Tsopano, Atate Akumwamba, ine ndakhala ndikuyankhula motalikitisa. Pali anthu amene akhala pano amene ali anthu a Muyaya, mmodzi aliyense wa ife. Mitu yathu ili yoweramitsidwira ku fumbi, kumene Inu munatichotsako ife; ndipo ngati Inu mutachedwe, ife tidzabwerera ku fumbi limenelo. Mizimu iyi ndi miyoyo imene ili mwa ife, iyenera kubwerera kwa Inu chifukwa cha Chiweruzo.

²⁵⁷ Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikupemphera kuti Inu mulemekeze Mawu Anu usikuuno. Ine ndayankhula za Inu, tsopano yankhulani kuti ine ndanena Choonadi, Ambuye. Ndine wantchito Wanu. Ine ndikudzipereka ndekha kwa Inu. Ndipo ngati pangakhale winawake munu, Ambuye, amene ali ndi chikhulupiriro cha mtundu umenewo, chimene chikhoza kubweretsa mawonetseredwe a Yesu Khristu; kudzasonyeza kuti chizindikiro chimene Iye analonjeza, chizindikiro chotsiriza kwa mpingo wa Amitundu, icho chikhala chikuchitika; mpingo wosankhidwa, monga gulu la Abrahamu, oitanidwa atuluke. Ife tikumuwona Billy Graham ndi amuna awo kumusi uko mu Sodomu, akuwaitana iwo atuluke; koma ife tikukumbukira Mmodzi yemwe anatsala ndi Abrahamu anawapatsa iwo chizindikiro china, kuti mwana wakudzayo anali pafupi. Ambuye, mutilole ife tiwone chizindikiro chimenecho, usikuuno, monga Munthuyo anali atatembenezira nsana Wake ku hema, ndipo anati, “Nchifukwa chiyani Sarah waseka?” Yesu anati izo zidzabwereza kachiwiri, basi kusanafike kudza kwa Mwana wa munthu; Mulungu anawonetseredwa mu thupi, mu mnofu wa munthu, kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera ndi Magazi a Yesu Khristu. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikupereka izi, inemwini, kwa Inu kwa utumiki Wanu. Yankhulani, Ambuye. Antchito Anu akumvetsera.

²⁵⁸ Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu waku Nazareti, ine ndikuwutenga mzimu uliwonse munu pansu pa ulamuliro wanga, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu, chifukwa cha ntchito za Iwo. [Winawake akuyamba kuyankhula mmalirime. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . ? . . .

²⁵⁹ Tsopano mulole Mzimu Woyera ugwire ntchito. Tsopano ndi zinthu zimene ine ndanena molondola, kapena kodi izo si zolondola? Kodi Iye akanalibe Khristu? Kodi Iye anasunga lonjezo Lake, za, “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi, Ine ndidzakhala pakati pawo”? “Kanthawi pang’ono, ndipo dziko kunjira uko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine” (puronauni yaumwini) “ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu. Ntchito zimene Ine

ndikuzichita, inunso mudzazichita; zochuluka kuposa izi, pakuti Ine ndikupita kwa Atate.” Kodi izo nzoona?

²⁶⁰ Ine ndikukuwona Kuwala kuja kutapachikika pa mtsikana wamng’ono, wachikuda apo. Iye akusinha. Ingokumbukirani, iye akhala bwino. Iwe wachokera kutali kwambiri ndi kuno. Iwe wayenera wadzipereka nsembe kuti uzibwera kuno usiku uliwonse, koma usachite mantha za mwanayo. Iwe wapeza chisomo ndi Mulungu. Iye anaitanidwa, usiku wina. Ingokhulupirira.

²⁶¹ Apa, kodi aliyense anayamba wakuwonapo Kuwala kumeneko? Kwezani dzanja lanu ngati inu munatero. Inu munachiwonapo chithunzi cha Iko. Kodi simukukuwona Iko? Yang’anani kuno. Yang’anani kuno. Kuwala kumeneko, mtundu wa amarodi, kwaima pomwe pano. Kodi inu simukukuwona Iko? Kukuyenda, pomwe apa.

²⁶² Iko kuli pa mkazi. Iye akuvutika ndi matenda a shuga. Iye wapemphera. Iye akukhulupirira. Mulungu, musalole kuti Iko kumusiye iye. Iye akuphonya Iko, motsimikiza basi. . . Akazi a Davis, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Ndi zimenezo pamenepo.

²⁶³ Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo, mmoyo wanga. Apa pali manja anga pamaso pa Mulungu. Mumufunse iye ngati zinthu zimenezo. . . Kodi izo nzoona, dona? Gwedezezi manja anu, monga *chonchi*, ngati izo ziri zoono. Tsopano kodi iye anamukhudza Ndani? Osati ine, iye ali mayadi twente kuchokera kwa ine. Koma iye wamukhudza Wansembe Wamkulu, Yesu Khristu. Mungokhala ndi chikhulupiriro. Musakaikire ayi. Kodi inu mukukhulupirira?

²⁶⁴ Apa, yang’anani kuno kachiwiri, apa pomwe. Mkazi wina akupemphera. Iye akuvutika ndi vuto la mmimba, chinachake chavuta ndi miyendo yakeyo. O Mulungu! Akazi a Cotton, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Landirani machiritso anu, Yesu Khristu wakupangani inu wamphumphu.

²⁶⁵ Mulungu Kumwamba akudziwa kuti ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo mmoyo wanga. Kodi iye anakhudza chiyani? Kodi ameneyo si Wansembe Wamkulu yemweyo? Nchifukwa chiyani inu mukukaikira? Musakaikire. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

²⁶⁶ Winawake yemwe amakhala kuno. Inu mupemphere. Khulupirirani. Iye ndi Mulungu,ponseponse.

²⁶⁷ Pali dona wakhala apa akupemphera. Iye sakudzipempherera yekha. Iye akumupempherera mwana wake. Iye ali ndi vuto la mmimba. Iye sali pano. Iye ali mu dera lina. Iye ndi wochokera ku mzinda wotchedwa Pontiac, Michigan. Musachite mantha. Iye anali ndi zilonda za mmimba, zoyambika chifukwa cha manjenje. Izo zamuchokera iye. Ameni. Chikhulupiriro chanu chinamukhudza Iye.

268 Kuti inu mukhoze kudziwa. Apa pakhala bambo pano, amene amasewera gitara iyi, chirichonse chimene icho chiri pano, akuvutika ndi vuto la mmimba, nayenso. Mdierekezi amaganiza kuti wakwanitsa kuchita izo, koma iye sanatero. Inu mwachiritsidwa, bwana. Yesu Khristu wakuchizani inu.

269 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? “Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.”

Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

270 Mnyamata wamng’ono apa wakhala, akumupempherera mkazi wake, ali ndi manja ake mmwamba. Iye akuvutika ndi chikhaliidwe cha mphumu. Ngati inu mukukhulupirira kuti Mulungu amuchiritsa iye, m’bale, iye achiritsidwa. Amen.

271 “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Afunsi anthu amenewo, ine sindinayambe ndawawonapo iwo mmoyo wanga.

272 Kumbuyo komwe kuno kwakhala mkazi wina. Iye ali ndi chotupa pa bere. Oh, iye asati aphonye izi! Akazi a Patterson, landirani machiritso anu. Imirani ku mapazi anu, perekani ulemelero kwa Mulungu. Chabwino. Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo, mmoyo wanga; Mulungu Kumwamba akudziwa zimenezo.

273 Nanga bwanji pa machira amenewo kumusi uko? Nanga bwanji mkazi pamenepo? Mwaweramitsa mutu wanu pansu, mkaziyo. Apo pakhala mkazi wakhala apo, iye ali pa machira. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, wantchito Wake? Pali Kuwala kwapachikika pa dona ameneyo. Iye akuvutika ndi vuto la mtima. Ngati mutagone pamenepo, inu mufa. Dzukani, mu Dzina la Yesu Khristu. Mutenge bedi lanu ndipo muzipita kwanu, ndipo inu muthana nalo vuto lanu la mtimalo.

274 Kodi inu mukumukhulupirira Mulungu? Ndi angati a inu mukumukhulupirira Iye? Mvetserani, abwenzi anga. Wamkulu kuposa Solomoni ali pano, Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu. Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Ngati imeneyo si ntchito imene Yesu Khristu anadzitsimikizira Iyemwini kuti ndi Mesiya! Kodi icho ndi chimene Lemba limanena? Nenani, “Ameni.”

275 Ndipo tiri pomwepo, inu, mukukumana ndi kusokonezeka kwa manjenje. Chokani kwa izo. Thawitsani moyo wanu. Thamangani msanga. Ziyikeni zinthu zimene ziri zakale zikhale zakale, ndipo muyang’ane kwa Mulungu. Ndinu mtumiki wa Uthenga. Inu, ine ndinayankhula nanu mmawa uno. Inu simunadziwe chimene icho chinali, ndipo ine sindinadziwe chimene icho chinali, koma ine ndachiwona icho tsopano. Inu mukubwera ku kusokonezeka. Mdierekezi akuyika chirichonse mmalingaliro anu, kuyesetsa kuti akupangitseni inu kuti mutembenuke, ngakhale kutsutsana ndi ine. Izo nzoona. Ndizo

PAKUTI ATERO AMBUYE. Iwalani zimenezo. Muuzeni iye kuti iye ndi wabodza. Landirani izo pakali pano, ndipo izo zikusiyani inu ndipo izo sizidzabwereranso kachiwiri. Inu mudzakhala munthu waufulu.

²⁷⁶ Ine ndikukutsutsani inu kuti mukhulupirire zinthu izi! Bamboyo anabwera kwa ine mmawa uno, kudzandifunsa. Ine sindimadziwa, koma ine ndikuziwona izo. Pomwe apa izo ziri patsogolo pake, tayang'anani pa mthunzi wakuda uwo ukungosunthira mkati ndi kunjira. Koma tsopano chinthucho chamuchokera iye. Uko nkulondola. Aleluya. "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

²⁷⁷ Pamene Mzimu Woyera uli pano, apa pali mipango. Tiyeni tipemphere, pamene inu mukugwira mu pemphero.

²⁷⁸ Atate Akumwamba, ife timaphunzitsidwa mu Baibulo, kuti iwo anatenga kuchokera mu thupi la Paulo Woyera, mipango ndi zovala, mizimu yonyansa inatuluka mwa anthu, ndipo iwo anachiritsidwa. Ndipo pamene ife tikuzindikira za Kukhalapo Kwanu pano, ife tikuzindikira kuti ife sitiri Paulo Woyera, koma Inu mukadali Yesu. Ndipo uyo sanali iye, poyamba pomwe, zimenezo munali Inu; chikhulupiriro mwa anthuwo, pamene iwo anamuwona iye akunenera ndipo anadziwa kuti Mulungu anali ndi iye. Ambuye, Inu mulemekeze mapemphero a anthu panonso lero, mwanjira yomweyo.

²⁷⁹ Wolemba wina anati, "Pamene Israeli anali panjira yake waku dziko lonlonjedwa, kuti Nyanja Yofiira inawadula iwo, mu njira kumene ya ntchito, waku dziko lonlonjedwa. Ndipo Mulungu anayang'ana pansu kupyolera mu Lawi la Moto limenelo, ndi maso okwiya; Nyanja Yofiira inachita mantha, inasunthira mmbuyo, ndipo Israeli anapitirira waku dziko lonlonjedwa."

²⁸⁰ Mulungu, usikuuno, anthu akufuna lonjezo limenelo, "Ine ndikanafuna pamwamba pa zinthu zonse mukanamachita bwino mu thanzi labwino." Ndipo matenda awadula iwo. Mulole Inu muyang'ane pansu usikuuno kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu, ndipo pamene mipango iyi ikaikidwe pa odwala, pokumbukira kudodza kwakukulu uku kwa Mzimu Woyera, wa Khristu akudziwonetsera Yekha pano kudutsa mthunzi wa kukaikira, Yesu yemweyo akutisonyeza ife kuti Iye akadali wamoyo ndipo anauka kwa akufa. Mulole matenda akawopsyzedwe pamene zizindikiro izi zikaikidwe pa odwala, mulole iye akathamangire mmbuyo ndi kusunthira kutali, ndipo anthu akachiritsidwe, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁸¹ Mwakachetechete. Baibulo ndi lolondola. Ndipo ngati Yesu walolera kubwera pano ndi kudzazipanga izi kuwonetseredwa kwambiri kwa inu, mwangwiro kwambiri, kudutsa gawo lililonse la kuwerenga maganizo, kupitirira gawo lililonse la kutengeka, chozizwitsa changwiro! Chozizwitsa ndi chinachake

chimene sichingakhoze kufotokozedwa. Ine ndikhoza kuwona pamene munthu akhoza kukhala—wolumala pang’ono pa phazi lake, ndipo akhoza kulumphira mmwamba, ndipo pansi pa kutengeka. Zabwino. Koma ndani angakhoze kumuuzwa iye zomwe iye wachita, ndi kumene iye akuchokerako, ndi zomwe zachitika, ndi zomwe ziti zidzakhale? Ndipo ine ndikukutsutsani inu; izo sizinaphonyepo nthawi imodzi, mu teni sauzande kuchulukitsa masauzande, kuzungulira dziko lapansi. Osati a . . .

282 Ife tiri nazo zotsanzira zambiri, ine ndikudziwa zimenezo. Zimenezo zikuyenera kubwera, kutsanzira kwa chithupithupi. Koma izo siziti. . . Izo zimangopangitsa Chinthu chenichenicho kuwala mwabwinoko; izo zimamupanga Yesu Khristu kukhala weniweni.

283 Apa Iye ali usikuuno! Iye ali pakati pathu, Mzimu Woyera womwewo umene inu munawulandira, ndipo Iye amakulolani inu kuti muziyankhula ndi malirime ndi kumachita zinthu zimene inu mwachitazi. Mzimu Woyera womwewo ukukupatsani inu chizindikiro cha Sodomu chija, kuti muchoke mu zinthu za mtundu umenewo, ora la kuwotchedwa kwa dziko lino liri pafupi. Bomba lagona kutsidyako ndi nambala pa ilo. Thawirani kwa Khristu, mwamsanga.

284 Iye ananenanso, mu Malemba, mawu otsiriza amene anagwa kuchokera pa milomo Yake, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

285 Ine ndiwona ngati inu mukhulupirire zimenezo? Ine ndikudabwa ngati ife tingayendetse wabwino, wakachitidwekachikale, mzere waku Arkansas wamsanga kuno, kwa miniti. Kodi inu mukhulupirira izo? Kodi inu mungafune mutawona zimenezo, manja atasanjikidwa pa inu? Kodi mukufuna kuti mukhale nazo zimenezo?

286 Ine sindikudziwa momwe tingayendetse iwo. Ine ndikukayika ngati ife tingakhoze kuchita zimenezo. Kodi inu mukukaikira zimenezo? Kodi inu mukuganiza kuti ife tingakhoze? [M’bale Samueli Johnson akuti, “Ine ndikukhulupirira ife tikhoza. Amen!”—Mkonzi]. Ine sindikudziwa momwe ife titi tichitire. Koma ife tikhoza kuyesera, ngati mungakhale molemekeza.

287 Mulole iwo amene ali mmenemo. . . Chiyani? Chigawo ndi chigawo. Chabwino, mulole iwo amene ali kumbuyo uko, amene agwirizira makadi apemphero amenewo, abwere kutsogolo kumene mu mzere umenewo apo. Gawo lakumanja.

288 Tsopano ine ndikufuna kuti inu mudziwe, abale anga, alongo, kuti inu simukusowa kuti mudikirire mlaliki winawake wapadera kuti abwere pamenepo. Ayi, ayi. Abusa anu ali nazo chimodzimodzi. Tsopano, iye—iye—iye mwinamwake

sangakhoze kukhala—kuti akhale ndi mphatso ya uneneri imeneyo; imeneyo amabwera mmodzi mu m’badwo. Koma, taonani, iye ali nawo maufulu womwewo kuti akupempherereni inu omwe ine ndikanati nditero. Kuzindikira za mumtima kumeneko sikumakuchiritsani inu; iko kumangokubweretserani inu chikumbumtima cha Mulungu, kuti muli mu Kukhalapo kwa Mulungu.

²⁸⁹ Koma mlaliki amapita mtawuni, amakachita kupemphera konse, kubatiza konse; ndiye anthu, pamene iye akuchoka, abusa ndiwo... Chabwino, anthu amaganiza kuti m’busa wawo si kanthu. Abusa anu ndi munthu wa Mulungu. Iye wakutsogolerani inu motetezeka mpaka apa; iye akhoza kukutengerani inu chitsogolo. Iye ndi munthu wolangizidwa ndi Mulungu.

²⁹⁰ Ndipo ine ndikufuna inu, mmodzi aliyense wa inu, ngati inu mubwere kudzadutsa mzere wa pemphero uwu ndipo inu simumakhulupirira izi, mukhale kunja kwa izo; inu mukhala mukuipiraipira. Koma ngati muzikhulupirira izo kwenikweni, pamene mukudutsa pansu pa manja odzozedwa a Mulungu, ine ndikufuna kuti inu muzipita kwanu mukuchitira umboni kwa mphamvu ya Mulungu; muzichoka pano, mukufuula ndi kumutamanda Mulungu, kuti izo zonse zatha. Ine ndikufuna kuti inu muchite zimenezo.

²⁹¹ Ine ndikufuna azibusa awa andithandizire ine. Oh, M’bale Moore, ndi M’bale Hooper, ndi ambiri a abale awa pano amene ine ndikuwadziwa, ndi gulu labwino ili la azibusa kuno, mungoima ndi kundipangira ine mzere wawung’ono mofola apa.

²⁹² Umu ndi momwe ife tinkachitira izo. Ine sindinachite izi kwa zaka. Koma pamene Mzimu Woyera ukadali pa ine (ine ndinangowona chinachake chikuchitika nthawi imeneyo basi.), pamene Iye akadali pano, ndipo pamene ine ndingathe, ndipo pamene... Iwo ali nako kudzoza komweko ndi ulamuliro womwewo. Ndizo zonse. Ife tiika manja pa odwala. Ndipo Baibulo linati, “Iwo adzayika manja pa odwala, iwo adzachira.” Baibulo linanena chomwecho. Amenewo ndi Mawu a Mulungu. Bwerani cha kuno, abale, bwerani cha kuno ndipo mudzapange mzere wofola apa. Ine ndiyima ndi abale awa.

²⁹³ Tsopano, pamene inu muzituluka, anthu inu pamalo awa, pamene mukupita panja, muzipita panja mukuzungulira nyumbayi, muzilowanso mkati pozungulira kuseri. Ndipo tsopano ine ndimufunsa winawake kuti aime pano, mwinamwake m’bale wamng’ono uyo pano, wamng’ono... Bwerani kuno, ndipo inu muziyang’ana mizere iyi, ngati mungathe, kapena m’bale wina amene angaime apa ndi kuwaitana iwo mwa zigawo.

²⁹⁴ Mulole atumiki tsopano, atumiki, antchito odzozedwa a Yesu Khristu, angoyima kumene motsatira apa.

295 Ine ndiri nawo abale angapo kuno amene ali ochokera ku Jeffersonville, ena a othandizana nawo anga ochokera ku mipingo yaing'ono yapaubale kuchokera ku Kachisi. M'bale Don Ruddell, kupambana kwakukulu popempherera odwala. Don, kodi inu muli pano? M'bale Junior Jackson, mlaliki wa Methodistine ndangomubatiza kumene mu Dzina la Yesu Khristu. Iye analandira Mzimu Woyera. Wina uyu anali mtumiki wa church of God. Ine ndikufuna inu abale amene mumapempherera odwala, kuzungulira Kachisi, mubwere, mudzaimu mu mzere uwu ndi abale awa.

296 Izo ziri bwino, sichoncho izo, m'bale? Izo nzabwino, sichoncho izo? Zedi. [Abale akuti, "Zedi!"] Eya. Chabwino, bwerani, mudzaimu pozungulira.

297 Alikuti M'bale Willard Collins? Mtumiki wina, mtumiki wa Methodistine, wangolandira kumene Mzimu Woyera, ndipo anabatizidwa. Ine ndikufuna kuti iye abwere.

298 Mnyamata wake wamng'ono, tsiku lina, anali akufa ndi—ndi nyamakazi, ndipo adokotala anati musamulole nkomwe iye kuti akweze mutu wake mmwamba mokwanira kuti ayike chubu mkamwa mwake. Ine ndinabwera kuchokera ku Tucson, kuti ndidzalalikire *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri*. Ndipo pamene iye anatero, iye anamunyamula mwana ameneyo kumuchotsa pa bedipo ndipo anamubweretsa iye kumeneko. Ndipo asanalowe nkomwe mkati, ndipo Mzimu Woyera unati, "PAKUTI ATERO AMBUYE. Umutengere mwanayo kunyumba, iye wachiritsidwa. Iye akasewera ndi mnyamata wanga wamng'ono." Ndi uyu m'bale waima pomwe pano tsopano. Mkazi wake ali muno.

299 Ine ndikuganiza Mike wakhala muno, iyemwini. Kulondola. Iwe uli pati, Mikey, iwe uli pati? Ndipo madokotala... Ndi uyo apo; chinsinsi. Adotolo anati mbweretseni... Akuluakulu azaumoyo anathamanga naye mwana ameneyo. Adokotala anapita ndipo anakamupima iye; iye anakanda mutu wake, anati, "Palibe chidutswa chimodzi cha izo mwa iye."

300 Ndi chiyani chimenecho? Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!

301 Abwenzi, chifukwa chimene ine ndawaitanira amuna awa, iwo ndi atumiki, iwo ndi azibusa, iwo ndi amuna amene anaitanidwa kuti adzapempherera odwala, chimodzimodzi monga ine ndiriri kapena munthu wina aliyense. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti abusa anu ali nawo ulamuliro woti azichita zimenezi. Inu simukusowa kuti muzimudikirira Oral Roberts, kapena Jack Jones, kapena ine, kapena wina aliyense. Yesu Khristu ndi wopezeka ponseponse; inu muzimukhulupirira Iye. M'busa wanu anaitanidwa kuti azichita zimenezo. Ngati simunabatizidwepo; ukatha msonkhano uno, muwafunse abusa anu, muzikonze ndi Mulungu. Ngati inu

simunalandire Mzimu Woyera; mupite ku mpingo wake, iye akakulangizani inu choti muchite.

³⁰² Tsopano pamene muzidutsa, muzipemphera. Ndipo ine ndikufuna munthu aliyense muno, munthu aliyense, ine ndikufuna kuti inu mupemphere. Ine ndikufuna inu muzingoguba kudutsa mzerewu. Ine ndiima pomwe pano ndi gulu ili la anthu, kumasanjika manja pa anthu awa. Abusa awa ayima apa ndi kumaitana mizere. Ndipo pamene inu muzidutsa, ndipo manja odzozedwa awa... Ine ndikupemphererani inu tsopano, ndipo iwo akupemphererani inu.

³⁰³ Ndipo pamene iwo aziyika manja pa inu, kumbukirani, ndizo, inu mwachiritsidwa basi monga inu mungapululumutsidwire. Baibulo, Ilo linati, “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Ndiro lonjezo la Mulungu. Iye achita zimenezo ngati inu mukukhulupirira zimenezo. Koma ngati simukukhulupirira izo, izo sizigwira ntchito. Ndipo Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Izo zatheka, pamene iwo akuyika manja pa inu, ngati inu mukukhulupirira izo.

³⁰⁴ Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi mukukhulupirira, usikuuno, kuti inu mwawona zenizeni basi monga momwe mayi gwape uja angakhoze kutulutsa, kumuwona Yesu Khristu akudziwonetsera Yekha pakati pathu? Ngati inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndiye, ndi Uyu apa.

³⁰⁵ Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano. Tsopano ili ndi pemphero langa kwa inu, ndi mtima wanga wonse:

³⁰⁶ Atate Akumwamba, ine ndimakukondani Inu. Ndinu Moyo wanga. Ndinu ziyembekezo zanga, Mulungu wanga, Mfumu yanga, Mchiritsi wanga, Wondisunga wanga. Osati zokhazo ayi, koma ine ndikufotokoza kumverera kwa Mkhristu wokhulupirira aliyense muno, ndicho chimene Inu muli.

³⁰⁷ Apa payima munthu, ena a iwo aima pano iwoeni, akudwala. Ine ndikudziwa iwo ali. Ine ndinawona Mzimu Wanu utapachikika pa iwo, mphindi pang’ono zapitazo. Podziwa atumiki odwala awo, koma mtima wawo ukutsatira osonkhana awo, anthuwo; apinyolitsa malo awo omwe, kuti adzaime pano mu mzere wa pemphero, kuti adzapempherere nkhosa zawo. Mulungu, amudalitse munthu ameneyo, adalitse mmodzi aliyense wa iwo.

³⁰⁸ Pamene ife taima pano ngati wokuimirani Wanu, usikuuno, wa Choonadi ichi, Choonadi cha Baibulo, mulole mmodzi aliyense wa amuna awa akhale odzozedwa kwambiri, ndipo Mzimu Woyera udza... Pamene iwo aziyika manja awo pa

anthu, kuti pakhale chikhulupiriro choterocho chikumukhudza munthu ameneyo mpaka iwo alandire mphatso yoperekedwa ndi Mulungu ya machiritso imene Inu munawalonjeza iwo, Ambuye. Ndipo mulole aliyense yemwe ati adutse, akhale wodzazidwa ndi chiyembekezo, kuti iwo adziwe kuti iwo akudutsa pansu pa mthunzi wa mtanda, pamene Magazi a Yesu Khristu akutetezera kuvomereza kwawo, ndi Kukhalapo Kwake kwakukulu kwaulemu kuli pano ndi ife tsopano, izo zikutsimikizira kuti Iye siali wakufa, Iye wauka kwa akufa, ndipo ali wamoyo pakati pathu. Ndiye mitima yathu izitentha pamene ife tizipita ku nyumba zathu zosiyanasiyana, usikuuno, kumati, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula kwa ife mkati mwa njirayi?” Ine ndikupempha kuti Mphamvu Yanu ipereke chikhulupiriro choterocho mu maminiti pang’ono otsatirawa, kwa anthu odwala awa, kuti pasakhale munthu wofooka pakati pathu.


³⁰⁹ Ine ndikumutsutsa mdierekezi aliyense amene wawamanga anthu awa, pa ulamuliro wa Mawu a Mulungu, ndi Kukhalapo kwa Yesu Khristu Amene anakhetsa Magazi Ake, kuti adzawapange Mawu aliwonse kukhala chenicheni kwa munthu aliyense amene angakhulupirire. Satana, iwe wagonjetsedwa, nthawi yako yayandikira, asiye anthu awa, mu Dzina la Yesu Khristu. Tuluka mwa iwo! Ife tikusunthira kuchita kwa Mulungu, pa kusanjika manja pa odwala, ndipo iwo achiritsidwa.

³¹⁰ Samuele, uziiyimba *Kungo Khulupirira*. Tikuyamba mzere wa pemphero. Aliyense mu pemphero tsopano. Aliyense, pemphero. [Mzere wa pemphero unakhala maminiti 11, mawu a M’bale Branham sakumveka. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu;
Chiyanjano cha malingaliro achibale
Chiri chonga chija Chakumwamba.

Pamene ife tisiyana,
Izo zimatipatsa ife kupweteka kwa mkati;
Koma ife tidzalumikizanabe mu mtima,
Ndi kuyembekeza kudzakumananso.

³¹¹ Atate Akumwamba, mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole kukhudzana uku kwa manja a wina ndi mzake, monga abale otumikira a Mawu a Mulungu, kupereke ukoma umene unamuukitsa Khristu kwa akufa, ndipo wamusunga Iye ndi ife kwa zaka thuu sauzande izi, mulole izo zimangirize. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . miyoyo kwa Muyaya, ndipo mulole Iwo uchiritse matenda pakati pathu. Ndipo mulole Dzina la Yesu Khristu. . . ? . . Mipango iyi ndi maphukusi awa, mulole mphamvu ya Mulungu ipume pa iwo, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

³¹² Tsopano mulole osonkhana onse, amene akukhulupirira ndi mtima wanu wonse, kuti Yesu Khristu atero, asunga Mawu Ake . . . Ngati Iye anasunga Mawu Ake kwa zaka thuu sauzande, ndipo anati izi zikanadzachitika pa nthawi yotsiriza, ndipo apa izo zachitika, Iye adzasunga Mawu Ake amene anati, “Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi inu mukuvomereza zimenezo? Ndiye tiyeni tikweze manja athu pamodzi ndipo timupatse Mulungu matamando . . . ? . . . 

63-0628E Wamkulu Kuposa Solomoni Ali Pano
Associated Brotherhood Of Christians Campground
Hot Springs, Arkansas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org